

Pemphero

Lopembedzera

HARVESTIME INTERNATIONAL INSTITUTE

Phunziro limeneri ndi gawo limodzi la maphunziro a **Harvest International Institute** ndipo cholinga chake ndi kukonzekeretsa okhulupilira kuti akatute zokolora zambiri zauzimu.

Mutu waukulu mumaphunzirowa ndikuphunzitsa zimene Yesu anaphunzitsa, zimene zinasandulitsa anthu wamba monga asodzi, otolera misonkho ndi ena kulalikirira Uthenga Wabwino ndi kuwonetsera mphamvu ya uthengawo mu nthawi yawo.

Bukuli ndi phunziro limodzi mwa maphunziro ambiri amene cholinga chake ndikuwakopa okhulupilira kuti akakonze dongosolo, kuyendetsa, ndi kubweretsa pamodzi anthu kuti Uthenga Wabwino ukalalikidwe.

© Harvestime International

Institute <http://www.harvestime.org>

ZAMKATI MWA BUKULI

	TSAMBA
Kagwiritsidwe Ntchito Ka Bukuli	4
Ndondomeko Zothandizira Kuphunzira Limodzi Pagulu	5
Chiyambi	6
Zolinga Za Phunziroli	7
1. Chiyambi Cha Pemphero	9
2. Pemphero Lopembedzera	18
3. Chuma Cha Uzimu Pa Kupembedzera	25
4. M'mene Mungapembedzerere	36
5. Zolepheretsa Kupembedzera Kochitachita	41
6. Kugwiritsa Ntchito Pemphero La Chitsanzo Popembedzera	45
7. Kupembedzera Chitsitsimutso	56
8. Kuyamba Ndi Kupita Chitsogolo	64
Zakumapeto 1: Mapemphero a mu Baibulo	72
Zakumapeto 2: Ndondomeko yophunzirira: Kupembedzera kwa m'Baibulo	78
Mayankho Amafunso Oziyesa Nokha	79

KAGWIRITSIDWE NTHCITO KA BUKULI

KAKONZEDWE KA BUKULI

Phunziro liri lonse limakhala ndi zinthu izi:

Zolinga: Izi ndi zimene mukuyenera kukwaniritsa kapena kudziwa pa mapeto pa phunziro. Welengani zimenezi musanayambe phunziro lanu.

Vesi Yotsogololera: Ndimeyi imatsindika mfundo yayikulu mu phunziro lathu.

Zopezeka mu Magawo: Gwiritsani ntchito Baibulo lanu kuti mufufuze mavesi amene sanalembedwe mu bukuli koma angotchulidwa.

Mayeso Odziyesa Nokha: Osathamangira kulemba mayeso musanamalize kuwerenga chaputala, komanso polemba musagwiritse ntchito Baibulo kapena bukuli polemba mayesowa. Mayankho amayesowa muwapeza kumapeto a bukuli.

Zophunzira Zowonjezera: Ndime imeneyi ikuthandizani kuti muwerenge mau Mulungu ndi kuzamitsa ukadaulo wanu pophunziro komanso kugwiritsa ntchito mu utumiki zimene mwa.

Mayeso Omaliza: ngati mwayamba kuphunzira phunziroli mukuyenera kulemba mayeso pamapeto a phunziroli ndipo mayesowo aperekedwa kwa aphunzitsi anu kuti mupatsidwe malikisi.

ZOWELENGA ZINA ZOFUNIKA POHUNZIRA PHUNZIROLI

Mudzafunikira Baibulo

NDONDOMEKO ZOTHANDIZIRA KUPHUNZIRA LIMODZI PAGULU

MKUMANO WOYAMBA

Kutsekulira: Yamabani ndi pemphero ndi kudziwana wina ndi mnzake ndipo ophunzira alembetse mayina.

Khazikitsani Ndongomeko Zapagulu: Musankhe amene atsogolere mkumano wanu, sankhaninso malo ndi masiku amene mudzikumana.

Mayamiko ndi Matamando: Yitanirani kupezeka kwa Mzimu Woyera pamene muchita mkumano wanu.

Gawani Mabuku Kwa Ophunzira: Awuzeni ophunzira dzina laphunziro, zolinga zake ndi dongosolo.

Perekani Nchito Yoyamba. Ophunzira ayenera kuwerenga ma chaputala amene apatsidwa ndikulemba mayeso odziyesa okha isanafike nthawi ya mkumano wina. Ndipo kuchuluka kwa machaputala amene adziphunzitsidwa pa mkumano uli onse kuzitengera kutalika kwa chaputala komanso kumvetsetsa kwa ophunzira.

MKUMANO WACHIWIRI NDI KUKUMANA KWINA PATSOGOLO

Kutsekulira: Tsekulirani ndi pemphero kenako lembani mayina awophunzira atsopano ndikuwapatsa buku lawo. Muyitane mayina a wophunzira amene abwera. Komanso osayiwala mayamiko ndi matamando kwa Mulungu.

Kukumbutsira: Yambani ndi kubwereza mwachidule zimene munaphunzitsa mu mkumano wanu womaliza.

Phunziro: Afunseni ophunzira ndemanga zawo kapena mafunso okhudza phunziro limene aphunzira komanso mmene angagwiritsire ntchito zimene aphunzira pamoyo wawo ndi utumiki.

Mayeso Odziyesa Nokha: Konzetsani mayeso amene ophunzira amaliza ndipo mukhonza kusankha kupereka mayankha kapena kuwachotsa mubukuli kuti ophunzira adzipezere okha mayankho.

Mayeso omaliza: Pamapeto pa maphunziro amenewa, gulu la ophunzira onse lidzapemphedwa kulemba mayeso omaliza ndipo aphunzitsi awonetsetse kuti ophunzira wina aliyense ali ndi buku laphunziroli.

CHIYAMBI

Mukuyamba ulendo wosangalatsa. Pa ma tsamba a bukulu muphonzira za chuma champhamvu cha uzimu chomwe chiri chopedzeka mu Thupi la Khristu, chimene chiri pemphero lopembedzera.

Mu phonzirori muphonzira chimene pemphero lopembedzera chiri ndi m'mene mungalichitire kuti likakhale lochitachita pogwiritsa ntchito zinthu (chuma) cha mphamvu cha uzimu chimene chaperekedwa pa cholinga ichi. Muphonzira kuti mupempherere chani, momwe mungathanirane ndi zolepheretsa za pemphero lopembedzera, ndi m'mene mungayambiri ndi kupita pachitsogolo.

Moyo wanu wa uzimu ndi utumiki siukakhalanso chimodzimodzi. Kodi mwakonzeka kuyamba ulendo wopita kumalo osngalatsa auzimu?

ZOLINGA ZA PHUNZIROLI

Pomaliza pa phunzirori mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kutanthauza pemphero.
- X Kufotokoza momwe pemphero limayankhidwira.
- X Kulemba mwachidule kufunika kwa pemphero mu moyo wa Yesu Khristu.
- X Kudzindikiri milingo ya pemphero.
- X Kudzindikira mitundu ya pemphero.
- X Kutanthauza pemphero lopembedzera.
- X Kufotokoza maziko a m’Baibulo a utumiki wa okhulupirira ngati opembedzera.
- X Kudzindikira Yesu Khristu ngati chitsanzo chathu pa kupembedzera.
- X Kufotokoza momwe mungapembedzerere.
- X Kufotokoza kufunika kwa kupembedzera
- X Kudzindikira chuma cha uzimu pa kupembedzera, chomwe chiri:
- X Mphamvu ndi ulamuliro wopatsidwa.
- X Kumanga ndi kumasula.
- X Dzina la Yesu.
- X Mwazi wa Yesu.
- X Kusala kudya.
- X Kugwirisa ntchito chumachi mu kupembedzera.
- X Kufotokoza m’mene mungapembedzerere.
- X Kulemba mwachidule mfundo za kupembedzera kochitahcita.
- X Kudzindikira zinthu zomwe mungapemberere.
- X Kugwiritsa ntchito malonjezano a Mulungu popembedzera.
- X Kudzindikira ndi kuchotsa zolepheretsa kupembedzera kochitachita.
- X Kudzindikira nthawi imene simukuyenera kupemphera.
- X Kupereka chitsanzo cha pemphero la chitsanzo.
- X Kufotokoza chifukwa chimene pemphero la Ambuye liri pemphero lopembedzera.
- X Kunena pemphero lachitsanzo osaonera.
- X Kugwiritsa ntchito pemphero lachitsanzo popembedzera.
- X Kutanthauza chitsitsimutso.
- X Kufotokoza momwe tingakonsekerere chitsitsimutso.
- X Kudzindikira pamene chitsitsimutso chikufunika.
- X Kudzindikira zizindikiro za chikhalidwe chobwerera m’buyo.
- X Kulemba mwachidule mfundo za m’Baibulo za chitsitsimutso.
- X Kudzindikira zolepheretsa za chitsitsimutso.
- X Kufotokoza m’mene mungagwiritsire ntchito “dongosolo la Mulungu ya chitsitsimutso” popembedzera chitsitsimutso.
- X Kukonza ndondomeko yakapempheredwe

- X Kupanga ndondomeko yakapempheredwe
- X Kupembedzera mayiko ena
- X Kudzindikira zovuta zomwe zikuyenera kugonjetsedwa
- X Kudzipereka nokha ku utumiki wa kupembedzera.

CHAPUTALA 1

CHIYAMBI CHA PEMPHERO

ZOLINGA:

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kutanthauza pemphero.
- X Kufotokoza momwe pemphero limayankhidwira.
- X Kulemba mwachidule kufunika kwa pemphero mu moyo wa Yesu Khristu.
- X Kudzindikiri milingo ya pemphero.
- X Kudzindikira mitundu ya pemphero.

VESI YOTSOGOLERA:

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu;

pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citseguldwa. (Mateyu 7:7-8)

CHIYAMBI

Chaputala ichi chikuyamba kukamba za phundirola la pemphero. Muphunira tanthauzo la pemphero ndi kufunikara komwe Yesu anaikidza pa pemphero. Muphunzira momwe pemphero limayankhiridwa ndi milingo yosiyanasiyana ndi mitundu ya pemphero.

TANTHAUZO LA PEMPHERO

Pemphero ndi kulumikidzana ndi Mulungu. Imatega njira zosiyana siyana koma imachitika pomwe munthu akulankhula ndi Mulungu ndi Mulungu kulankhula ndi munthu. Pemphero limafotokodzeredwa ngati:

Kuyitanira pa dzina la ambuye:	Genesis 12:8
Kufuulira kwa Mulungu:	Masalimo 27:7; 34:6
Kutsendera chifupi kwa Mulungu:	Masalimo 73:28; Ahebri 10:22
Looking up:	Masalimo 5:3
Kutsanurira mitima kwa Mulungu:	Masalimo 62:8

Kutsanurira moyo kwa Mulungu:	1 Samuel 1:15
Kufuulira kumwamba:	2 Mbiri 32:20
Kumupempha Mulungu:	Eskodo 32:11
Kumusaka Mulungu:	Yobu 8:5
Kusaka nkhope ya Ambuye:	Masalimo 27:8
Kuchita mapemphezere:	Yobu 8:5; Yeremiya 36:7

Pemphero sikungoyankhula ndi Mulungu kokha, kuti kumvetseranso. Pemphero ndi kulumikidzana, ndipo kulankhula kwa munthu m' modzi yekha sikuenga nthawi. Mukamapemphera, mudziyembekedzera kuti Mulungu akulankhulani. Nthawi zambiri amachita idzi kudzera mu Mawu ake olembedwa kapena “mawu odekha” omwe amalankhula ku mitima yanu. Nthawi zina amakupatsana masomphenya kapena kutanthauzira mu uzimu wanu zomwe mwapemphera mu chilankhula chakumwamba cha pemphero.

Osangothamanga kupereka zopempherera zanu kwa Mulungu ndi kutsiriza pemphero lanu. Lolani kuti naye akulankhuleni. Apereka mayankho ku mafunso anu, chitsogodzo cha tsiku lomwe liri nkudza, ndi kukuthandidzani kuyika moyenera zinthu zofunikira pa moyo wanu. Nthawi zina amakupatsani uthenga wapaderadera wa chilimbikitso kuti mukagawire wina yemwe mukumupempherera.

Mukamapemphera, palibe makhalidwe oyenera ovomerezedwa. Mutha kupemphera pomwe

Mutayima:	1 Mafumu 8:22; Marko 11:25
Titawerama:	Masalimo 95:6
Titagwada:	2 Mbiri 6:13; Masalimo 95:6; Luka 22:41; Machitidwe 20:6
Kugwa pa nkhope yanu:	Numeri 16:22; Yoswa 5:14; 1 Mbiri 21:16; Mateyu 26:39
Kutambatsula manja:	Yesaya 1:15; 2 Mbiri 6:13
Kukweza manja:	Masalimo 28:2; Maliro 2:19; 1 Timoteo 2:8

MOMWE PEMPHERO LIMAYANKHILIDWA

Baibulo limaonetsera ku pemphero limayankhidwa:

Nthawi zina pompo pompo:	Yesaya 65:24; Danieli 9:21-23
Nthawi zina limachedwerapo:	Luka 18:7
Kutsiyana ndi zokhumba zathu:	2 Akorinto 12:8-9
Kupyola zoyembekedera zathu:	Yeremiya 33:3 Aefeso 3:20

MOYO WA YESU WA PEMPHERO

Pemphero likuyenera kukhala lofunikira kwa ife chifukwa linali lofunikira kwa Ambuye Yesu. Yesu ndi chitsadzo chatu cha pemphero lopemphedzera. Werengani zitsanzo zotsatirazi za moyo wapemphero wa Yesu:

YESU ANATENGA PEMPHERO KUKHALA LOFUNIKIRA:

- Amamphera nthawi ina ili yonse: Luka 6:12-13
- Pemphero linali lofunikira kuposa chakudya: Yohane 4:31-32
- Anaphunzitsa akuphunzira ake kupemphera: Mateyu 6:9-113

PEMPHERO LINATSATANA NDI CHOCHITIKA CHINACHILICHOTSE CHOFUNIKIRA PA MOYO WAKE

- Pa ubatizo wake: Luka 3:21-22
- Pa ulendo wake woyamba wa utumiki: Marko 1:35; Luka 5:6
- Atsanankhe ophunzira ake: Luka 6:12-13
- Atsanadyese ndi atatha kudyetsa anthu 5,000: Mateyu 14:19,23; Marko 6:41,46; Yohane 6:11,14-15
- Pomwe amadyetsa anthu 4,000: Mateyu 15:36; Marko 8:6,7
- Chibvomerezo cha Petro chisanachitike: Luka 9:20
- Mawalitsidwe a Yesu asanachitike: Luka 9:28,29
- Pamanda a Lazalo Yohane 12:27-28
- Pomwe amadalitsa ana: Mateyu 19:13
- Kwa Petro: Luka 22:32
- Pakupereka Mzimu Woyera: Yohane 14:16
- Pa njira yaku Emau: Luka 24:30-31
- Atsanakwere kukwera kunka kumwamba: Luka 24:50-53
- Pa omutsatira iye: Yohane 17
- Atsanayesedwe: Mateyu 26:26-27 Marko 14:22-23; Luka 22:17-19

MILINGO YA PEMPHERO

Pali milingo itatu ya pemphero: Kupempha, kufuna, ndi kugogoda:

Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu;

pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citsegulidwa. (Mateyu 7:7-8)

Kupempha ndi mlingo woyambirira wa pemphero. Kumatanthauza kupereka zopempha kwa Mulungu ndi kulandira yankho pompopompo. Kuti mulandire, mukuyenera kuti mupemphe

...mulibe kanthu, cifukwa simupempha. (Yakobo 4:2)

Kufuna ndi mlingo wakuya wa pemphero. Uwu sim lingo omwe mayankho amakhala a pompopompo ngati mlingo wa kupempha. Anthu 120 omwe anakumana muchipinda chapamwamba omwe anali kupemphera kotsalekeka ndi chitsanzo cha kufuna. Anthu awa amafuna kukwaniritsidwa kwa onjezano la Mzimu Woyera ndipo anapitiriza kufuna mpakana yankho linafika (Machitidwe 1-2).

Kugogona ndi mlingo wakuya. Ndi pemphero lomwe liri lokakamidza ngati yankho silikubwera. Ikuwonetseredwa pa fanizo lomwe Yesu anakamba pa Luka 11:5-10. Komanso likuwonetseredwa ndi Daniel yemwe anapitiridza “kugogoda” ingakhale samaona mayankha chifukwa Satana anagwira mayankho ochokera kwa Mulungu (Daniel 10).

MITUNDU YA PEMPHERO

Paulo anaitana okhulupirira onse kuti akapemphere “mapemphero onse” (Aefeso 6:18). Ma Baibulo onse amati “kupemphera ndi mitundu yonse ya mapemphero.” Izi zikutanthauza mitundu yosiyanasiyana ya mapemphero yomwe ili:

1. CHIYAMIKO NDI CHILEMEKEZO:

Mumalowa mukupezeka kwa Mulungu ndi Chiyamiko ndi chilemekezo:

Lowani ku zipata zace ndi ciyamiko, Ndi ku mabwalo ace ndi cilemekezo: Myamikeni; lilemekezeni dzina lace. (Masalmo 100:4)

Kulemekeza ndi kupereka ulemu. Kuyamika ndi kuthokoza ndi kuonetsa kuyamikira osati chifukwa cha zimene Mulungu wachita zokha koma chifukwacho cha zimene Mulungu ali. Mukuyenera kumulemekedza (kulambira) Mulungu mu Mzimu ndi muchoonadi.

Koma ikudza nthawi, ndipo tsopano iripo, imene olambira oona adzalambira Atate mumzimu ndi m'coonadi; pakuti Atate afuna otere akhale olambira ace.

Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira iye ayenera kumlambira mumzimu ndi m'coonadi. (Yohane 4:23-24)

Kulambira mulungu mu choonadi zikutanthauza kuti mukulambira Iyi malingana ndi zomwe zabvumburutsidwa mu Mawu a Mulungu. Kumulambira mu Uzimu ndikulambira kudzera mu mphamvu ya Mzimu Woyera, kuchokera mkati mwanu, kuika Iye kukhala oyamba pa zinthu zina ziri zonse. Pamene mukulambira mu Uzimu, mumamulola Mzimu yoyera kuti ayendetse

kulambira kwanu. Inu simumagwiritsa ntchito njira za zuthi pa kulambira. Simumangobweredza zonenerra kapena pemphero ndi malingaliro anu ali kwina.

Koma, mumatsegula mtima wanu ndi malingaliro anu, ndikupereka matamando ndi mayamiko kwa Iye mu mawu anu. Nthawi zina, Mzimu Woyera amatenga gawo lonse ndipo mumayamba kulambira mu “malilime ena” achilankhulo chanu cha pemphero.

Chiyamiko ndi chilemekedzo chitha kukhala ndi:

Nyimbo:	Masalimo 9:2,11; 40:3; Marko 14:26
Mayamiko omveka:	Masalimo 103:1
Kufuula:	Masalimo 47:1
Kukweza manja mwamba:	Masalimo 63:4; 134:2; 1 Timoteo 2:8
Kuyimba mmanja	Masalimo 47:1
Zida zoyimbira nyimbo:	Masalimo 150:3-5
Kuimirira:	2 Mbiri 20:19
Kuwerama:	Masalimo 95:6
Kuvina	Masalimo 149:3
Kugwada	Masalimo 95:6
Kugona pansi:	Masalimo 149:5

2. KUZIPEREKA:

Ili ndi pemphero lopereka moyo wanu ndi chifuniro kwa Mulungu. Imaphatikadza pemphero la kudzipatula ndi kudzipereka kwa Mulungu, ndi zolinga zake.

3. ZOPEMBEDZERA:

Mapemphero azopembedzera ndi zopempha. Zopempha zikuyenera kuchitidwa molingana chifumiro cha Mulungu monga momwe zabvumbutsiridwa mu Mawu ake olmbedwa. Zopembedzera zitha kukhala pa mulingo wopempha, kufuna, kapena kugogoda. Kupembedzera kumatanthauza “kumupempha Mulungu m’ malo mwa chosowa.”

4. KUBVOMEREZA NDI KULAPA

Pemphero la kubvomereza ndi kulapa ndi kupempha chikhululukiro cha machimo.

Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:9)

5. KUPEMPHERERA:

Kupempherera ndi pemphero lopempherera anthu ena. Munthu opempherera ena ndi amene amatenga malo a munthu wina kapena kupempha m'malo mwa wina. Iri ndi pemphero lomwe bukuli likufotokoza.

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

2. Tanthauza pemphero.

3. Fotokozani momwe pemphero limayankhidwira.

4. Lembani mwachidule kufunika kwa pemphero mu moyo wa Yesu Khristu.

5. Dzindikirini milingo ya pemphero.

6. Lembani mitundu yisanu ya pemphero yomwe yakambidwa mu chaputala ichi.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

1. Umu ndi momwe mungapempherere dziko lonse lapansi

Lolemba	Pemphererani Asia
Lachiwiri:	Pempererani Europe
Lachitatu:	Pemphererani Africa
Lachinayi:	Pemphererani North America
Lachisanu:	Pemphererani Latin America
Loweruka:	Pemphererani Oceania (Mayiko azilumba)
Lamulungu:	Pemphererani dziko lonse lapansi

2. Werenganinso mavesi otsatirawa ndipo muyetse kupemphera malingana ndi momwe mavesiwo akufotokozerana:

Mutayima:	1 Mafumu 8:22; Marko 11:25
Titawerama:	Masalimo 95:6
Titagwada:	2 Mbiri 6:13; Masalimo 95:6; Luka 22:41; Machitidwe 20:6
Kugwa pa nkhope yanu:	Numeri 16:22; Yoswa 5:14; 1 Mbiri 21:16; Mateyu 26:39
Kutambatsula manja:	Yesaya 1:15; 2 Mbiri 6:13
Kukweza manja:	Masalimo 28:2; Maliro 2:19; 1 Timoteo 2:8

3. Werenganinso mavesi otsatirawa ndipo muyese kulambira ndi kutamanda Mulungu mu njira zosisiyanasiyana zomwe Mavesiwa akufotokoza:

Nyimbo:	Masalimo 9:2,11; 40:3; Marko 14:26
Mayamiko omveka:	Masalimo 103:1
Kufuula:	Masalimo 47:1
Kukweza manja mwamba:	Masalimo 63:4; 134:2; 1 Timoteo 2:8
Kuyimba mmanja	Masalimo 47:1
Zida zoyimbira nyimbo:	Masalimo 150:3-5
Kuimirira:	2 Mbiri 20:19

Kuwerama:

Masalimo 95:6

Kuvina

Masalimo 149:3

Kugwada

Masalimo 95:6

Kugona pansa:

Masalimo 149:5

CHAPUTALA 2

PEMPHERO LOPEMBEDZERA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kutanthauza pemphero lopembedzera.
- X Kufotokoza maziko a m’Baibulo a utumiki wa okhulupirira ngati opembedzera.
- X Kudzindikira Yesu Khristu ngati chitsanzo chathu pa kupembedzera.
- X Kufotokoza momwe mungapembedzerere.
- X Kufotokoza kufunika kwa kupembedzera.

VESI YOTSOGOLERA:

kucokera komwekoakhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa iye, popeza ali nao moyo wace cikhaliire wa kuwapembedzera iwo. (Ahebri 7:25)

CHIYAMBI

Mu phunziro lapitalo mwaphunzira kuti **kupembedzera** ndi kupemphera m’ malo mwa anthu ena. Munthu opempherera ena ndi amene amatenga malo a munthu wina kapena kupempha m’ malo mwa wina. Mukamapembera chomwechi, **mukupembedzera:**

“kupemphedzera kutha kutanthauzidwa ngati pemphero langwiro, lakhama lomwe munthu amadandaulira Mulungu m’ malo mwa munthu wina kapena anthu ena omwe akufunikira kupedzeka kwa Mulungu.” (Baibulo la Full Life)

Iri ndi pemphero lomwe bukuli likufotokoza. Mu phunziro iri muphunzira maziki a m’Baibulo a kupembedzera ndi chitsanzo chathu cha kupembedzera, Ambuye Yesu Khristu. Muphunziranso momwe mungapembedzerere komanso chifukwa chimene uli utumiki wofunikira.

MAZIKO A M’BAIBULO A KUPEMBEDZERA

Maziko athu a m’Baibulo mu utumiki wa okhulupirira a Chipangano Chatsopano wa pemphero lopembedzera ndi mayitanidwe athu ngati ansembe akwa Mulungu. Mawu a Mulungu amalengedza kuti ndife ansembe oyera mtima (1 Petro 2:5), mbadwa wosankhidwa (1 Petro 2:9), ndi ufumu wa ansembe (Chibvumbulutso 1:5).

Maziko ofuna kumvetsetsa mayitanidwe a unsembe akupezeka mu chitsanzo cha ansembe achi Levi mu Chipangano Chakale. Udindo wa ansembe unali woyima **pamaso** ndi **pakati**. Amayima pamaso pa Mulungu potumkira ndi nsembe ndi zopereka. Wansembe amayimaso pakayi pakati pa Mulugu wolungama ndi anthu ochimwa powabweresa limodzi pa malo a nsembe ya mwazi.

Ahebri 7:11-19 ikufotokoza kusiyana kwapakati pa unsembe wa Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Unsembe wa Chilevi wa Chipangano Chakale umaperekedwa kuchokera ku

m’badwo kupita ku m’badwo kudzera ku m’badwo wa fuko la Levi. “Unsembe wa Melikizedeki” omwe wakambiidwa mu ndimeyi, ndi “ndondomeko yatsopano” ya unsembe wa uzimu womwe Ambuye Yesu ndi Wansembe Wankulu. Ukuperekedwa kwa ife kudzera mu mwazi Wake ndi kubadwanso kwathu wa uzimu ngati zolengedwa zatsopano mwa Khristu.

CHITSANZO CHA OPEMBEDZERA

Baibulo limaonetsa kuti cholinga cha Mulungu potumiza Yesu chinali choti Iye azagwire ntchito ngati opembedzera.

Ndipo Iye anaona kuti palibe munthu, nazizwa kuti palibe wopembedzera; cifukwa cace mkono wace wace unadzitengera yekha cipulumutso; ndi cilungamo cace cinamcirikiza. (Yesaya 59:16)

Yesu amayima pamaso pa Mulungu ndi pakati pa Iye ndi ndi munthu wochima, monga momwe wansembe wa Chipangano Chakale amachitira.

Pakuti pali Mulungu mmodzi, ndi Mtetezi mmodzi pakati pa Mulungu ndi anthu, ndiye munthu, Kristu Yesu, (1 Timoteo 2:5)

... Kristu Yesu ndiye amene adafera, inde makamaka, ndiye amene adauka kwa akufa, mene akhalanso pa dzanja lamanja la Mulungu, amenenso atipempherera ife. (Aroma 8:34)

kucokera komwekoakhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa iye, popeza ali nao moyo wace cikhalire wa kuwapembedzera iwo. (Ahebri 7:25)

Yesu amabweretsa pamodzi munthu wauchimo ndi Mulungu wolungama pamodzi pa malo a nsembe ya mwazi ya uchimo. Mwazi wa nyama siwofunikiratsa ngati momwe zinaliri mu Chipangano Chakale. Titha kufika pamaso pa Mulungu malinga ndi maziko a mwazi wa Yesu omwe unakhetsedwa pa mtanda wa Kavale kuti ukuchotse machimo. Chifuka cha mwazi wa Yesu, mutha kufika pamaso pa Mulungu opanda mantha (Ahebri 4:14-16).

Yesu anali opembedzera pomwe anali pano pa dziko. Anapempherera iwo omwe anali odwala ndi ogwidwa ndi ziwanda. Anapempherera ophunzira ake. Anapemphereranso inu pomwe anapempherera aliyense yemwe angazakhulupirire pa Iye. Yesu anapitiriza utumiki wopembedzera pomwe anakwera kupita Kumwamba. Ndippo pano amagwira ntchito ngati opembedzera Kumwamba.

MOMWE MUNGAPEMBEDZERERE

Ngati opembedzera omwe tikusatira kagwiridwe ka ntchito ka ansembe a Chipangano Chakale ndi ndondomeko ya Chipangano Chatsopano cha Yesu, timayima pamaso pa Mulungu ndi pakati pa Mulungu ndi munthu wauchimo. Kuti tikakhale oyima “pakati” ochitachita tikuyenera kuyamba kaye kuyima “pamaso” pa Mulungu kuti yikakuze ubale ofunikira kuti tikakwanirise udindowu.

Numeri 14 ndi chitsanzo chimodzi chachikulu cha pemphero la kupembedzera yolembedwa mu Baibulo. Mose anali othejera kuyima pakati pa Mulungu ndi munthu wauchimo chifuma amayima pamaso pa Mulungu ndipo anakuzza ubale wake ndi Mulungu. Numeri 12:8 imakamba kuti Mulungu amalankhulana ndi Mose ngati bwenzi kulankhulana ndi bwenzi lake osati kudzera mu masomphenya ndi maloto ngati momwe amachitira ndi aneneri ena.

Ngati okhulupirira a Chipangano Chatsopano sitipereka nsembe za nyama ngati mu Chipangano Chakale. Timayima pamaso pamulungu ndikupereka nsembe zauzimu za matamando (Ahebri 13:5) ndi nsembe za miyoyo yathu (Aroma 12:1). Ndi pamaziko a ubale wathu ndi Mulungu omwe umatipangisa kuti tiyime “pakati” pa Mulungu ndi anthu ena, kugiwira ntchito ngati nkhalapakati ndi opembedzera m'malo mwawo.

Petro anagwiritsa ntchito mawu awiri pofuna kufotokodza utumiki wa unsembewu: “Woyera ndi Wachifumu.” Chiyero chimafunikira kuti muntu akayime pamaso pa Ambuye (Ahebri 12:14). Ife timakwanisa chifukwa cha chilungamo cha Khristu osati chilungamo chathu. Ufumu umafotoloza za ulamulilo wa chifumu womwe waperekedwa kwa ife ngati mamembala a “banja la chifumu,” ndi kukhala ndi kuthejera kofika mu chipinda wa mpando wa chifumu wa Mulungu.

Nthawi zina unsembe wopembedzera umachitika ndikumvetsetsa. Izi zimachitika ngati mukupembedzera anthu ena muchilankhulo chanu ndipo mukumvetsetsa zomwe mukunena:

Ndidandaulira tsono, poyambayamba, kuti acitike mapembedzo, mapemphero, mapembedzero, mayamiko, cifukwa ca anthu onse;

Cifukwa ca mafumu ndi onse akucita ulamuliro ... (1 Timoteo 2:1-2)

Nthawi zina, kupembedzera kumachitika ndi Mzimu Woyera. Zitha kuchitika ndi kubuula chifukwa cha kulemedwa kwa uzimu. komanso zitha kuchitika ndi malilime osaziwika. Izi zikamachitika, Mzimu Woyera umalankhula kudzera mwa inu kupemphera kwa Mulungu malingana ndi chifuniro cha Mulungu:

Ndipo momwemonso Mzimu athandiza kufoka kwathu; pakuti cimene tizipempha monga ciyenera, sitidziwa; koma Mzimu mwiniatipempherera ndi zobuula zosatheka kuneneka; (Aroma 8:26)

Pakuti iye wakulankhula lilime salankhula ndi anthu, koma ndi Mulungu; pakuti palibemunthu akumva; koma mumzimu alankhula zinsinsi. (1 Akorinto 14:2)

Inu simumvetsetsa kupembedzera uku ndi malingaliro anu, koma ndi mulingo wakuya wa pemphero lopembedzera komando wochitachita chifukwa umachitika “molingani ndi chifuniro cha Mulungu.” Malingaliro ndi zolinga zanu sizisintha mapemphero omwe apempheredwa ndi Mzimu Woyera kudzera mwa inu mu malirime osaziwika.¹

¹ Pofuna kupeza uthenga woonjedzera pa kulankhula mu malirime ena pezani phunziro la Harvestine International Institute lotchedwa “*Utumiki wa Mzimu Woyera.*”

KUFUNIKIRA KWA KUPEMBEDZERA

Kupembedzera ndikofunika kwambiri chifukwa cha kutsindikiza komwe Yesu anayika pa iwo pa utumiki wake wa dziko lapansi. Kufunika kwake kunalembedwanso mu Baibulo omwe umakwaniritsa nkhani za anthu omwe anakumana ndi zotsatira zamphamvu kudzera mu kupembedzera kochitachita.

Mukudzera mukupembedzera kochitachita, mutha kupita muuzimu kwina kuli konse pa dziko lapansi. Mapemphero anu alibe zophinja za kutalika kwa malo chifukwa amafikira mayiko onse osafikiridwa ndi kufikira kupyozza mu malire a mitundu, zikhalidwe komanso za ndale. Inu muntha kukhuza tsogola la munthu kapena dziko lonse. Inu mutha kukwanisa kupulumusa miyoyo ya amuna ndi akazi, anyamata ndi asungwana ndi kukudza Uthenga Wabwino wa Ufumu wa Mulungu pa dziko lonse lapansi pomwe mukupembedzera mu pemphero.

MAFUNSO OZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera.

2. Tanthauzirani pemphero lopembedzera.

3. Fotokozerani maziko a m'Baibulo a utumiki wa okhulupirira ngati opembedzera.

4. Kodi ndi ndani yemwe ali chitsanzo cha kupembedzera?

5. Fotokozani momwe mungapembedzerere.

6. Fotokozani kufunika kwa kupembedzera.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)
ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Yohane 17 ndi chitsanzo chimodzi cha pemphero lopembedzeralomwe lalembedwa m'Baibulo. Gwiritsani nchitho ndondomeko yotsatirayi pofuna kuwerenga pempheroli:

Yesu anazipempherera iye mwini:

Yohane 17:1-5

Lembani mwachidule zopempha Zake:

Yesu anapempherera ophunzira omwe anali nawo:

Yohane 17:6-19

Lembani mwachidule zopempha zake pa ophunzira ake:

Yesu anapempherera ophunzira ake amtsogolo:

Yohane 17:20-23

Lembani zopempha zimene Yesu anapempherera ophunzira ake amtsogolo:

Yesu amalidza pemphero lake:

Yohane 17:24-26

Lembani mwachidule m'mene Yesu anamalidzira pemphero lake:

Kodi chokhumba chake chenicheni ndi chiti?

Kodi anawonetsera chani kwa omutsatira Iye?

Kodi akufuna kuti “mwa iwo” akhale chani? _____

CHAPUTALA 3

CHUMA CHA UZIMU PA KUPEMBEDZERA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kudzindikira chuma cha uzimu pa kupembedzera, chomwe chiri:
- X Mphamvu ndi ulamuliro wopatsidwa.
- X Kumanga ndi kumasula.
- X Dzina la Yesu.
- X Mwazi wa Yesu.
- X Kusala kudya.
- X Kugwirisa ntchito chumachi mu kupembedzera.

VESI YOTSOGOLERA

Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)

CHIYAMBI

Mulungu wapereka chuma chochuluka pa utumiki wa kupembedzera omwe ife tayitanidwirako. Mu phunziro ili muphunziro m'mene mungagwiritsire ntchito chuma chimenechi chomwe chiri, mphamvu ndi ulamuliro wopatsidwa, kumanga ndi kumasula, Dzina la Yesu, mwazi wa Yesu ndi kusala kudya.

MPHAMVU NDI ULAMULIRO WOPATSIDWA

Pamene tikupembedzera mu pemphero timakhala kuti tikulimbana ndi m'dani, Satana, pa miyoyo ya amuna ndi akazi, anyamata ndi asikana, mitundu, ndi adzitsogoleri a uzimu ndi ndale. Sitimachita idzi ndi kuthekera kapena mphamvu zathu, koma ndi mphamvu ndi ulamuliro wa uzimu womwe wapatsidwa kwa ife ndi Yesu:

Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)

Pali kutsiyana pakati pa ulamuliro ndi mphamvu. Onani chitsanzo cha muthu wapolisi. Ali ndi batchi ndi unifolomu zomwe ziri zizindikiro za ulamulo. Ulamuliro wake umabwera chifukwa cha udindo womwe ali nawo ndi boma. Chifukwa si onse omwe amapereka ulemu ku ulamuliro, apolisi ena amatenga chida cha nkondo ndipo chidacho ndi mphamvu yake. Ulamuliro wanu pa m'dani umachokera kudzera mwa Yesu Khristu ndi udindo womwe muli nawo mwa Iye ngati okhulupirira. Mphamvu yanu pa m'dani imachokera kwa Mzimu Woyera.

Ndipo onani, Ine nditumiza pa inu lonjezano la Atate wanga; koma khalani inu m'mudzi muno, kufikira mwabvekedwa ndi mphamvu yocokera Kumwamba. (Luka 24:49)

Ngati wapolisi, mukuyenera kukhala ndi ulamuliro komanso mphamvu kuti mukakhale ochitachita mu kupembedzera, chifukwa mukumenya nkondo ya uzimu ndi Satana. Okhulupirira amalandira ulamuliro pakudzera mu kubadwatso kwatsopano ndi udindo wawo mwa Kristu koma ena safika ndikulandira mphamvu ya Mzimu Woyera yomwe ikuyenera kugwirdzana ndi ulamuliro kuti mukapembedzere mochitachita.

Satana ali ndi mphamvu zochepa koma alibe ulamuliro. Yesu anatipatsa mphamvu ndi ulamuliro pa mphamvu zonse za Satana. Mphamvu yomwe Yesu anapereka ndi mphamvu yomwe ikuyenera kugwiritsidwa pa zolinga zoyenera:

MPHAMVU PA M'DANI:

Muli ndi ulamuliro opembedzera mu pemphero kwa iwo omwe akufuna machiritso ndi mamasulidwe:

Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)

MPHAMVU PA TCHIMO:

Muli ndi ulamuliro opembedzera iwo omwe akufuna chipulumutso:

Zocimwa za anthu ali onse muwakhulukira, zikhulukidwa kwa iwo; za iwo amene muzigwiritsa, zagwiritsidwa. (Yohane 20:23)

MPHAMVU YOKUDZA UTHENGA WABWINO:

Muli ndi ulamuliro wopempherera ogwira ntchito kuti akakulitse Uthenga Wabwino.

Pomwepo ananena kwa ophunzira ace, Zotuta zicurukadi koma anchito ali owerengeka. (Mateyu 9:37)

KUMANGA NDI KUMASULA

Mawu oti “kumanga” amachokera ku mawu achi Heberi oti *osar* kutanthauza “kumanga, kuyang'anira.” Mawuwa timawagwiritsa ntchito powonetsera kumanga mahatsi ndi mabulu (2 Mafumu 7:10).

Zonena za Yesu pa Mateyu 12:28-29 ndi zatanthauza lalikiru:

Koma ngati Ine ndimaturutsa ziwanda ndi mphamvu yace ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulungu unafika pa inu.

Kapena akhoza bwanji munthu kulowa m'banja la munthu wolimba, ndi kufunkha akatundu ace, ngati iye sayamba kumanga munthu wolimbayo? ndipo pamenepo adzafunkha za m'banja lace. (Mateyu 12:28-29)

Ndikosatheka kutenga katundu wa munthu wolimba ngati sayamba kumanga munthu wolimbayo. Yesu, polankhula za munthu wolimba, amakamba za Satana. Akatundu omwe akuyenera kutengedwa kwa iye ndi akatundu ake amtengo wapatali, anthu otayika omwe amangidwa ndi iye, kuphatikidza iwo omwe “ali ndi ziwanda.”

Yesu anapereka mphamvu kwa okhulupirira ya kumanga ndi kumasula:

Ndidzakupatsa mafungulo a Ufumu wa Kumwamba; ndipo cimene ukamanga pa dziko lapansi cidzakhala comangidwa Kumwamba: ndipo cimene ukacimasula pa dziko lapansi, cidzakhala comasulidwa Kumwamba. (Mateyu 16:19)

Yesu anaphunzitsa kufunika komanga mizimu yoyipa musanayituluse, koma mfundo zomanga ndi kumasula zimapitirira kuposa kungotulusa ziwanda. Muntha kumanga mphamvu ya mdani kuti isagwire ntchito mu moyo wanu, banja lanu ndi m'dera lannu. Mutha kumasula amuna ndi akazi ku nsinga za tchimo, maganizo, ndi kukhumudwitsidwa ndi m'dani. Mu nyengo ina iriyonse... vuto lina lirilonse, chophinja chinachirichonse... pali mfungulo la uzimu. funguloyi ndi kumanga ndi kumasula kudzera mu pemphero lopembedzera.

DZINA LA YESU

Dzina la Yesu ndi ulamuliro omwe ife timapembedzerapo. Yesu analonjeza:

Ngati mudzapempha kanthu m'dzina langa, ndidzacita. (Yohane 14:14)

... Indetu, indetu, ndinena kwa inu, Ngati mudzapempha Atate kanthu, adzakupatsani inu m'dzina langa. (Yohane 16:23)

Ndipo zizindikilo izi zidzawatsata iwo akukhulupirira; M'DZINA LANGA adzaturutsa ziwanda; adzalankhula ndi malankhulidwe atsopano;

Adzatola njoka, ndipo ngakhale akamwa kanthu kakufa nako, sikadzawapweteka; adzaika manja ao pa odwala, ndipo adzacira. (Marko 16:17-18)

Mukuyenera kupemphera, kulalikira, kuphunzitsa, kubatiza, kutulutsa ziwanda, kuchilitsa odwala, ndi kupambana mphamvu zonse za Satana kudzera mu dzina la Yesu. Dzina la Yesu ndi la mphamvu kuposa dzina lina lirironse:

Pamwamba pa ukulu wonse, ndi ulamuliro ndi mphamvu, ndi ufumu, ndi dzina liri lonse lochedwa, si m'nyengo yinoya pansu pano yokha, komanso mwaiyo ikudza. (Aefeso 1:21)

Mwa icinso Mulungu anamkwezetsa iye, nampatsa dzina limene liposa maina onse, Kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansu pa dziko,

Ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate. (Afilipi 2:9-11)

MWAZI WA YESU

Mwazi wa Yesu ndi chuma china champhamvu cha uzimu chomwe chimatipangisa kuti tipembedzere. Ndikudzera mu mwazi Wake ife tiri ndi mwayi wofika pamaso pa Mulungu Atate:

Ndipo pokhala naco, abale, cilimbikitso cakulowa m'malo opatulika, ndi mwazi wa Yesu,

Pa njira yatsopano ndi yamoyo, imene adatikonzera, mwa cocinga, ndico thupi lace;

Ndipo popeza tiri naye wansembe wamkuru wosunga nyumba ya Mulungu;

Tiyandikire ndi mtima woona, m'cikhulupiriro cokwanira, ndi mitima yathu yowazidwa kuicotsera cikumbu mtima coipa, ndi matupi athu osambitsidwa ndi madzi oyera;

Tigwiritse cibvomerezo cosagwadera ca ciyembekezo cathu, pakuti wolonjezayo ali wokhulupirika. (Ahebri 10:19-23)

Malo “opatulika” ndi malo amene Mulungu amakhalako. Ife sitifika pamaso pa Mulungu pakudzera mu miyambo ya chipembedzo kapena njira zovuta. Timafika podzera mu mwazi wa Yesu Khristu.

Phunziro la mwazi ndi ulusi wofiila omwe ukuyenda mu Baiibulo lonse kuyambira ku Genesis kufikira ku Chibvumbulutso. Baibulo limatiphunzitsa kuti moyo wa munthu uli m'mwazi wake (Levitiko 17:11,14) Chifukwa mphoto ya uchimo ndi imfa (Aroma 6:23) ndipo chifukwa choti moyo wa munthu uli m'mwazi, Mulungu anakhadzikitsa mfundo yoti kukhulukiridwa kwa machimo kumachokera pa kukhetsedwa kwa mwazi kokha.

Ndipo monga mwa cilamulo zitsala zinthu pang'ono zosayeretsedwa ndi mwazi, ndipo wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka. (Ahebri 9:22)

Mulungu anapanga nsembe yoyamba ya mwazi mu Munda wa Edeni Adamu ndi Hava atachima pomwe anapha zinyama ndikuwaveka zikopa zomwe zimayimirira chilungamo cha Khristu. Kufunikira kwa nsembe ya mwazi kumaonetseredwa kwambiri mu nkhani ya Kaini ndi Abeli, pangano la m'dulidwe ndi a Islayeri ndi miyambo yachi Levi mu Chihema. Mu Chipangano Chakale mwazi wa zinyama umaperekedwa ngati nsembe kawirikawiri pamene muntu wachimwa. Ahebri 8 ikukamba za ndondomekoyi ndipo akuitcha kuti “pangano lakale.”

Mu Chipangano Chatsopano Mulungu anatuma Yesu kuti akakhetse mwazi wake kwa anthu onse. Mwazi wake umakambidwa ngati “pangano latsopano” (Marko 14:24) ndipo ndi mkhalapakati wa pangano latsopano (Ahebri 8:6). Izi zikupangisa kuti pangano lakale kuti lithe, izi zikutathauza kuti sikoyeneranso kuti mwazi wa zinyama uziperekedwa ngati nsembe ya tchimo.

kapena mwa mwazi wa mbuzi ndi ana a ng'ombe, koma mwa mwazi wa iye yekha, analowa kamodzi ku malo opatulika, atalandirapo ciombolo cosatha. (Ahebri 9:12)

Ahebri 9:24 imaonetsa kuti mwazi wa Yesu umalampirankhulira ndi chomwe umalankhula chimapereka phindu la moyo wa muyaya kwa ife. Pamene Paulo anatiuza kuti “tigwiritse cibvomerezo (Ahebri 10:23), ikugwirizana ndi mavesi omwe akambidwa m’buyomu omwe akuonetsera kuti tiri ndi ufulu ofika chifupi ku malo Opatulika.

Mumalowa mukupezeka kwa Mulungu ndi pemphero momga momwe munapulumsidwira, pakubvomereza phindu la mwazi wa Yesu:

kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka:

Pakuti ndi mtima munthu akhulupira kutengapo cilungamo; ndi m'kamwa abvomereza kutengapo cipulumutso. (Aroma 10:9-10)

Mulungu amagwira ntchito malingana ndi chibvomerezo chanu chimene chiri ndi ulamuliro chifukwa chili ndi maziko a umbozi wa mwazi wa Yesu. Mwazi umakamba zoti inu mutha kulowa mu malo opatulika tsopano lino kumene Mulungu amakhala ndi kutumikira kudzera pakupembedzera.

KUSALA KUDYA

Chinthu china chofunikira pa kupembedzera kochitachita ndi kusala kudya. Kusala kudya, kukutanthauza kuti kukhala osadya kanthu. Kusala kudya ndi chinthu chimodzi chomwe chimativomereza kuti ndife otumikira a Mulungu (2 Akorinto 6:3-10). Pemphero ndi kusala kudya kumachitika mu Mpingo woyamba (Machitidwe 14:23) ndipo Paulo anatirimbikitsa mtima kuti “tizipereke” ku ichi (1 Akorinto 7:5).

MITUNDU YA KUSALA:

Baibulo limatiuza za mitundu iwiri ya kusala. Kusala kosadya kapena kumwa kalikonse. Chitsanzo cha ichi chikupezeka pa Machitidwe 9:9. Kusala kwapadera ndi pamene chakudya china sichikudyedwa. Chitsanzo cha ichi chiri pa Danieli 10:3.

ZITSANZO ZA M’BAIBULO ZA KUSALA KUDYA:

-Kapolo wa Abrahamu anasala chakudya pamene amafuna mkazi woyenera ya Isaki (Genesis 24:33.)

-Mose anasala kwa masiku 40 pamene amalandira mabvumbulutso a chilamulo ndi chihema (Eskodo 34).

-Hana anasala pofuna mwana (2 Samueli 1:7-8)

-Nehemiya anasala pofuna kubwezeretsedwa kwa Yerusalemu (Nehemiya 1:4)

-Ayuda anasala pofuna chipulumutso potsatira lamulo la imfa la Hamani (Estere 4)

-Mzinda wonse wa nineve unasala povomereza utheka wakulapa wa Yona (Yona 3:5-10)

- Davide anasala asanatenge Ufumu womwe anapasidwa ndi Mulungu (1 Samueli 31)
- Danieli anasala kwa masiku 21
- Yehosafati analengeza kusala kudya asanapite kukamenya nkondo (2 Mbiri 20:3).
- Ezra anamemeza ana onse a Israyeli kuti asale (Ezra 8-9)
- Yesu anasala anasanayambe utumiki wake (Mateyu 4)
- Paulo mtumwi anasala atangotembenuka mtima kumene (Machitidwe 9).
- Inali nthawi yakusala pamene Petro analandira ntchito yokagawa Uthenga Wabwino ndi anthu Amitundu ndipo Koneliyasi anali okonzeka kulandira chibvumbulutso (Machitidwe 10)
- Ophunzira anali akupemphera ndi kusala pamene Mzimu Woyera anapatula Paulo ndi Banaba ku utumiki (Machitidwe 13:2).

CHOLINGA CHA KUSALA KUDYA:

Kusala kudya sikusinthana Mulungu. Kumasinthana inuyo. Mulungu amakhala nanu malingana ndi ubale wanu ndi Iye. Mukasinthana, momwe Mulungu amagwirira ntchito ndi inu kumasinthana. Simumasala kuti mukasinthana Mulungu chifukwa Mulungu sasinthana. Kusala kudya kumasinthana m'mene Mulungu amagwirira ntchito ndi inu. Werengani buku la Yona ngati chitsanzo cha ichi mu mzinda wa Ninevi.

Tsiku lina pomwe Ophunzira a Yesu analephera kubweresa chithandidzo kwa mwana wozaza ndi ziwanda, Yesu anafotokoza kuti “mtundu uwu” sukhoza kutuluka ndi kanthu kena konse, koma ndi pemphero ndi kusala kudya (Marko 9:29). Pali nyembgo zina m'moyo zomwe simungalimbane nazo pokhapokha mutapemphera ndi kusala kudya. Mochulukira pamene dziko likupita kumapeto, tizikumana ndi nyengo zoterezi, zomwe nyengo zowawisa zomwe sitinakumanepo nazo. Chipambano chathu pa zinthu izi kuzaonetsera kufunikira kwa kusala kudya

Pali zolinga za uzimu za kusala kudya. Ndikofunikira kuti mukamvetsetse zolingazi. Ngati mungasale ndi zolinga zolakwikwa kapena opanda cholinga chenicheni, kusala kwanu sikuzakhala kwa phindu. Werengani zitsanzo zotsatirazi. Zikuonetsera kuti anthu anasala:

- | | |
|--|-------------------|
| -Pakuvomereza uthenga ochokera kwa Mulungu: | Yona 3:5 |
| -Pakuyesedwa munthawi ya muchipululu: | Luka 4:1 |
| -Pamene pamasowekera chibvumbulutso kuchokera kwa Mulungu: | Danieli 9:3-4 |
| -Pofuna kupanga Chiganizo: | Machitidwe 13:3-4 |
| -Popereka chopempha pamaso pa anthu aulamuro: | Estere 4:16 |
| -Pokonzekera kukalimbana ndi ziwanda: | Marko 9:29 |
| -Pozichepesa iwe mwini: | Masalimo 35:13 |
| -Polapa mchimo: | Yoweli 2:12 |
| -Podyasa osauka, kuthupi ndi kuuzimu: | Yesaya 58:7 |

-Pofuna kumvedwa ndi Mulungu:

2 Samueli 12:16,22
Yona 3:5,10

MLINGO WA KUSALA:

Mlingo womwe mumasalira zimatengera ndi momwe Mulungu akulankhulira mu mzimu wanu. Anthu kukutsogozani kuti musale kw aka nthawi kochepa kapena kwa masiku ochuluka. Mukukumbukira nkhani ya Esau ndi Yakobo? Yakobo amakodza chakudya cha iye yekha koma anzikaniza yeka kuti apeze ukulu.

Ngati simunasalepo yambani kusala posadya chakudya cha m'mawa chokha. Kenako mutha kuyesa kusala tsiku lonse. Kenako mutha kuonjezera kusala kwa masiku angapo. Nthawi zonse muzimwa madzi ngati mukusala kwa masiku ambiri. Mutha kukhala opanda chakudya koma madzi amafunikira kuti thupi lizigwirabe ntchito bwinobwino.

KUSALA KWA GULU NDI KWA INU NOKHA:

Kusala ndi kwa inu mwini ndi Mulungu. Kukuyenera kuchitika mwachinsinsi osati modzitamandira:

Ndipo pameneponse musala kudya, musakhale ndi nkhope yacisoni, ngati onyengawo; pakuti aipitsa nkhope zao, kuti aonekere kwa anthu kuti alimkusala kudya. Indetu ndinena kwa inu, Iwo alandiriratu mphotho zao.

Koma iwe, posala kudya, dzola mutu wako, ndi kusamba nkhope yako:

kuti usaonekere kwa anthu kuti ulikusala kudya, koma kwa Atate wako ali m'tseri: ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe. (Mateyu 6:16-18)

Adzitsogoleri atha kulengeza kusala kwa gulu ndikupempha kuti mpingo wonse usale:

Ombani lipenga m'Ziyoni, patulani tsiku losala, lalikirani msonkhano woletsa. (Yoweli 2:15)

KUSALA KOSANKHIDWA KWA MULUNGU:

Yesaya 58 akufotokoza za kusala “kosankhidwa.” Kusala kosankhidwa ndi Mulungu ndi:

-Pamene mungazichepese nokha pamaso pa Mulungu: Vesi 5

-Kumasula nsinga za zoipa: Vesi 6

-Kumasula zomanga goli: Vesi 6

-Kuleka otsenderezedwa amuke mfulu: Vesi 6

-Kochitidwa ndi zolinga zabwino ndi kuonetsera ntchito zabwino: Vesi 7

ZOTSATIRA ZA KUSALA KUDYA:

Mukamasala, chinthu choyamba chimene chimachitika ndichakuti Mulungu amayamba kuzibvumbulutsa yekha kwa inu. Atate anati, “Pamenepo udzaitana, ndipo Yehova adzayankha; udzapfuula ndipo Iye adzati, Ndine pano” (Yesaya 58:9). Zotsatira zina zimene zakambidwa pa Yesaya 58 ndi:

-Chiwalitsiro: Vesi 8 ndi 10 akulengeza kuti nyengo za moyo wanu za mumdima zizawala ngati masana. Pamene ena azawona ngati azimitsa kuunika kwanu wa uzimu, pomwepo kuunika kwako kudzawalitsa monga m'mawa.

-Chitsogozo: Vesi 11 ikulonjeza kuti “ndipo Ambuyo azakutsogolerani posalekai.”

-Kupereka: Vesi 11 ikulengeza kuti Mulungu “adzakhutitsa moyo wako m'chirala.” (Izi zitha kukhudzana ndi nyengo za kuthupi ndi uzimu.) Vesi 11 ikukambazo za chuma cha uzimu chosatha. Inu mudzakhala ngati “munda wothirira madzi,” ndi “kasupe wamadzi amene madzi ake saphwa konse.”

-Kupereka mphanvu: Vesi 11 likulengeza kuti Mulungu “adzalimbitsa mafupa ako” ndipo vesi 8 likunena kuti “kuchira kwako kudzaonekera msanga msanga.”

-Kubwedzeretsedwa: Vesi 12 ikuonetsa kuti inu ndi mbewu yanu ya uzimu “mudzamanga malo akale abwinja; udzautsa maziko a mibadwo yambiri; udzachedwa Wokonza pogumuka, Wakubwezera njira zakukhalamo.”

CHUMA CHA KUPEMBEDZERA

Okhulupirira ali ndi zinthu zamphanvu za uzimu zothandizira kuti kupembedzera kukhale kochitachita. Pamene mwaphunzira mu chaputala ichi, izi zikuphatikidza:

- Mphanvu ndi ulamuliro wopatsidwa.
- Kumanga ndi kumasula.
- Dzina la Yesu.
- Mwazi wa Yesu.
- Kusala kudya.

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera.

2. Fotokozani kusiyana kwapakati pa mphamvu ya uzimu ndi ulamuriro.

3. Kodi kumanga chinthu muuzimu zikutanthauza chani?

4. Kodi kumasula chinthu mu uzimu zikutanthauza chani?

5. Kodi ndi vesi yanji yomwe imatipasa ulamuriro womanga ndi kumasula?

6. Fotokozani chifukwa chimene dzina la Yesu ndi la mphamvu kwambiri mu kupembedzera.

7. Kodi mwazi wa Yesu umagwira ntchito yanji mu kupembedzera.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Dzina la Yesu ndi ulamuliro omwe ife timapembedzerera kwa Mulungu. Werengani ndandanda wa mayina Ake pofuna kukuza chidziwitso chanu cha mphamvu yolandira mu dzina la “Yesu.”

Mkhalapakati	1 Yohani 2:1
Wamphamvu zonse	Chibvumbulutso 1:8
Woyamba ndi wotsiriza	Chibvumbulutso 21:6
Ameni	Chibvumbulutso 3:14
Oyamba/Omaliza chikhulupiriro chathu	Ahebri 12:2
Obwadwa kwa Mulungu	1 Yohane 5:18
Okonedwa	Aefeso 1:6
Nthambi	Zekariya 3:8
Mkate wa Moyo	Yohane 6:48
Mwala wa pangodya	1 Petro 2:6
Khristu	Yohane 1:41
Khomo	Yohane 10:9
Emanueli	Mateyu 1:23
Mwana wa Nkhosa wa Mulungu	Yohane 1:29
Kuunika kwa Dziko	Yohane 8:12
Mkate wa Moyo	Yohane 6:51
Ambuye Mulungu wa Mphamvu	Chibvumbulutso 4:8
Ambuye wa onse	Machitidwe 10:36
Ambuye Chilungamo chathu	Yeremiya 23:6
Chikondi	1 Yohane 53:3
Mesiya	Danieli 9:25
Woyeletsetsa	Danieli 9:24
Mbuye	Mateyu 23:10
Nazala	Mateyu 2:23
Mulungu yekhayowanzeru	1 Timoteo 1:17
Pasaka wathu	1 Akorinto 5:7
Wamankhwala	Luka 4:23
Kalanga wa Ntendere	Yesaya 9:6
Nkhala pakati	Aroma 3:25
Opulumutsa	Yesaya 59:20
Kuukaso ndi moyo	Yohane 11:25
Kapolo wachilungamo	Yesaya 53:11
Thanthwe	1 Akorinto 10:4
Mpulumutsi wa dziko lonse	1 Yohane 4:14
M’busa	Yohane 10:11
Mwana wa Mulungu	Aroma 1:4
Mwana wa Munthu	Machitidwe 7:56
Mwana wa Mariya	Marko 6:3
Mwala	Mateyu 21:42

Maziko olimba
Mphunzitsi
Choonadi
Mpesa
Njira
Wodabwisa
Mawu a Mulungu

Yesaya 28:16
Yohane 3:2
Yohane 14:6
Yohane 15:1
Yohane 14:6
Yesaya 9:6
Chibvumbulutso 19:13

CHAPUTALA 4

M'MENE MUNGAPEMBEDZERERE

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kufotokoza m'mene mungapembedzerere.
- X Kulemba mwachidule mfundo za kupembedzera kochitahcita.
- X Kudzindikira zinthu zomwe mungapemberere.
- X Kugwiritsa ntchito malonjezano a Mulungu popembedzera.

VESI YOTSOGOLERA:

Ndipo uku ndi kulimbika mrima kumene tiri nako kwa iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa cifuniro cace, atimvera; ndipo ngati tidziwa kuti atimvera ciri conse ticipempha, tidziwa kuti tiri nazo izi tazipempha kwa iye. (1 Yohane 5:14-15)

CHIYAMBI

Pemphero likuyenera kuperekedwa mwa chikhulupiro ndi chifuniro cha Mulungu:

Ndipo uku ndi kulimbika mrima kumene tiri nako kwa iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa cifuniro cace, atimvera; ndipo ngati tidziwa kuti atimvera ciri conse ticipempha, tidziwa kuti tiri nazo izi tazipempha kwa iye. (1 Yohane 5:14-15)

Mu phunziro iri muphunzira zomwe Baibulo limaphunzitsa pa m'mene mungapembedzerere ndi zinthu zomwe mungadzippedzere. Komanso muphunzira m'mene mungakhazikitsire pemphero lanu pa malonjezano a Mawu a Mulungu.

M'MENE MUNGAPEMBEDZERERE

Muone zitsanzo zotsatirazi mu Baibulo. Ndime zimenezi zikupereka malangizo a m'Baibulo pa kupembedzera:

- | | |
|--|---------------------|
| -Pembero likuyenera kuchitika kwa Mulungu: | Masalimo 5:2 |
| -Pemphero silimakhala laphindu chifukwa cholonkhula zochulukira: | Mateyu 6:7 |
| -Kupemphera ndi chidziwitso | Aefeo 6:18 |
| -Kupemphera mu Mzimu mu malirime: | Aroma 8:26; Juda 20 |
| -Kupemphera pa malo a m'tseri: | Mateyu 6:6 |
| -Pempherani nthawi zonse: | Luka 21:36 |
| | Aefeso 6:18 |
| -Kupemphera kwa Atate mu dzina la Yesu: | Yohane 14:13-14 |
| -Kudikirala m'mapemphero: | 1 Petro 4:7 |
| -Kupemphera pogwiritsa ntchito pemphero lachitsanzo: | Mateyu 6:9-13 |
| -Kupemphera ndi mzimu wokhululuka: | Marko 11:25 |

-Kupemphera ndi mtima wozichepetsa:	Mateyu 6:7
-Nthawi zina kumapemphera ndi kusala kudaya:	Mateyu 17:21
-Kupemphera molimbika mtima:	Yakobo 5:16; Akolose 4:12
-Kupemphera kuzipereka kwa Mulungu:	Luka 22:42
-Gwiritsani ntchito njira zomangira ndi zomasula mu pemphero:	Mateyu 16:19

MFUNDO ZA KAPEMBEDZEDWE KOCHITACHITA

Zotsatirazi ndi mfundo za kapembedzedwe kochitachita zomwe zatengedwa kuchokera ku mavesi ali mwambamo:

1. Mutamandeni Mulungu chifukwa cha chimene iye ali ndi mwayi wokhala nawo mu utumiki wabwino monga Ambuye Yesu (Ahebri 7:25). Mutamandeni Mulungu cha mwayi wogwirizana naye mu zochitika za anthu kudzera mu Pemphero.
2. Onetsetsani kuti mtima wanu uli woyera pamaso pa Mulungu pakumupatsa Mzimu Woyera nthawi yokutsutsani, ngati pali tchimo lomwe sirinabvomerezedwe (Masalimo 66:28; 29:23-24)
3. Vomeredzani kuti simungapemphere popanda chitsogozo ndi mphamvu ya Mzimu Woyera (Aroma 8:26). Mumufunse Mulungu kuti akutsogolereni ndi Mzimu Woyera, mukhulupirire ndi chikhulupiriro kuti amachitadi, ndi kumuthokoza Iye (Aefeso 5:18).
4. Menyanani molimbika ndi Satana. Mufikireni motsutsana naye kudzera mu Dzina la mphamvu zonse la Ambuye Yesu Christu ndi “lupanga la uzimu” --Mawu a Mulungu (Yakobo 4:7).
5. Ifani ku maganidzo anu, zokhumba zanu, ndi zophinja zomwe mukumva kuti mupemphere (Miyambo 3:5-6; 28:26; Yesaya 55:8).
6. Mutamandeni Mulungu tsopano ndi chikhulupiriro chifukwa mtsokhanao wa mapemphero omwe mukuyerana kukhala nawo. Ndi Mulungu wa chidwi ndipo achiti chinthu chogwiridzana ndi khalidwe Lake.
7. Yang'anirani kwa Mulungu moyembekedzera, kumvetsera chitsogozedwe chake (Masalimo 63:5; Mika 7:7; Masalimo 81:11-13).
8. Mu kuzichepetsa ndi muchikhulupiriro, lankhulani zimene Mulungu wabweretsa mu malingaliro anu, pokhulupirira (Yohane 10:17). Pitirizani kumufunsa Mulungu chitsogodzo, ndikuyembekedzera kuti Iye akupatsani inu. Achita ndithu (Masalimo 32:8).

9. Ngati kuli kotheka, khalani ndi Baibulo lanu pafupi ngati Mulungu angakupaseni chitsogodzo kapena chitsimikizo kuchokera mu Baibulo (Masalimo 119:10-15).
10. Pamene Mulungu wasiya kupereka zinthu mu malingaliro anu kuti muzipempherere, malidzitsani pakumutamanda ndi kumuyamika chifukwa cha zithu zonse zome Iye wachita, ndikuzikumbutsa nokha Aroma 11:36 “Cifukwa zinthu zonse zicokera kwa iye, zicitika mwa iye, ndi kufikira kwa iye. Kwa Iyeyo ukhale ulemerero ku nthawi zonse. Amen.”²

ZIMENE MUKUYENERA KUPEMBEDZERA

Werengani zitsanzo zotsatirazi za m’Baibulo zomwe zikuonetsera zinthu zimene mukuyenera kupembedzera:

-Mtendere wa Yerusalemu:	Masalimo 122:6
-Ogwira ntchito m’ munda:	Mateyu 9:38:38; Luka 10:2
-Kuti musalowa m’ mayesero:	Luka 22:40-46
-Adani anu:	Luka 6:28
-Oyera mtima onse:	Aefeso 6:18
-Odwala:	Yakobo 5:14
-Wina ndi mzake:	Yakobo 5:16
(Mumachimwa ngati simukupemherera anthu ena:	1 Samueli 12:23)
-Anthu onse, mafumu, ndi uwo aulamuliro:	1 Timothy 2:1-4
-Zosowa zathu za tsiku ndi tsiku:	Mateyu 6:11
-Nzeru:	Yakobo 1:5
-Chikhulukiro:	Mateyu 6:12
-Kuti chifuniro ndi Ufumu wa Mulungu ukhazikike:	Mateyu 6:10
-Mpumuli ku zowawa:	Yakobo 5:13
-Umodzi pa Thupi la Khristu:	Yohane 17:20-21
-Mpungo womwe ukuzudzidwa pa dziko lapansi:	Ahebri 13:3

KUPEMBEDZERA NDI MALONJEZANO

Mulungu amayankha mapemphero malingana ndi chifuniro chake ndipo chifuniro chake chikubvumbulutsidwa mu malonjezano omwe alembedwa mu Mawu ake. Ngati inu simukupempha malingana ndi malonjezanowa pemphero lanu siriyankhidwa.

Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukacimwaze pocita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)

Ndizofanana ndi momwe kholo limakhalira ndi mwana wake. Palibe kholo limene limapereka chirichonse chimene mwana wake wapempha. Amanena momveka bwino kuti achita zina koma zina satha kuchita. Kudzera mu malire amenewa kholo limayankha zopempha za mwana wake.

² Mfundo za kupembedzera mochitachita zatengedwa kuchokera ku *1992 Personal Prayer Diary*, (Settle, Washington: Achinyamata a utumiki, 1991)

Izi zirinso chomwechi ndi Mulungu. Watipasa malonjezano ake ndipo amapanga maziko a pemphero. Phunzirani zomwe Mulungu walonjeza ndipo pempherana molingana ndi malonjezanowa. Njira imodzi yochitira izi ndikupita mu Baibulo ndikulunjika pemphero lanu molingana ndi malonjezanowa. Mukamapemphera lonjezano, inu mumalengeza Mawu a Mulungu kwa Iye. Ichi ndi chitsanzo:

“Zikomo Mulungu chifukwa mukudziwa chomwe ndikufuna ngakhale ndisanapemphe (Mateyu 6:8). Ndikudza kwa inu mu dzina la Yesu, podzindikira mphamvu ya dzina limeneri (Yohane 14:14). Ndikupempherera kuti ogwira ntchito m'munda adzutsidwe kuti akakudze Ufumu wa Mulungu (Mateyu 9:38)...”

Awa ndi zitsanzo zochepa za malonjezano a m’Baibulo. Malonjezanowa akulunjika pa phunziro la pemphero:

- | | |
|--|------------------------------|
| -Atate amaziwa chomwe mukufuna inu musanapemphe: | Mateyu 6:8 |
| -Ngati awiri azagwirizane mu pemphero, izayankhidwa: | Mateyu 18:19 |
| -Zinthu zonse ndi zotheka ndi Mulungu: | Mateyu 19:26;
Luka 18:27 |
| -Pemphero lophatikidza ndi chikhulupiriro ndi lochitachita: | Mateyu 21:22;
Marko 11:24 |
| -Mukapempha mu dzina la Yesu, chidzachitika: | Yohane 14:14 |
| - Pemphero la munthu wolungama likhoza kwakukuru m'macitidweace. | Yakobo 5:16 |

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera.

2. Kodi munthu angapembedzere bwanji mu pemphero?

3. Kodi tingapembedzere zinthu ziti mu pemphero?

4. Lembani mwachidule mfundo za kupembedzera kochitahcita zomwe mwaphunzira mu chaputalachi.

5. Fotokozani momwe mungagwiritsire ntchito malojezano a Mulungu popembedzera.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

CHAPUTALA 5

ZOLEPHERETSA KUPEMBEDZERA KOCHITACHITA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kuzindikira ndi kuchotsa zolepheretsa kupembedzera kochitachita.
- X Kuzindikira nthawi imene simukuyenera kupemphera.

VESI YOTSOGOLERA:

Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukacimwaze pocita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)

Ngati mukufuna kuti mupembedzere bwino mukuyenera kudzikira zolepheretsa kupembedzera kochitachita ndipo mudzichote kumoyo wanu.

ZOLEPHERETSA KUPEMBEDZERA KOCHITACHITA

Werengani mavesi otsatilawa omwe amabvumbulutsa zolepheretsa kupembedzera kochitachita:

- | | |
|---|--|
| -Tchimo la mtundu wina uli wonse | Yesaya 59:1-2; Masalimo 66:19;
Yesaya 1:15; Miyambo 28:9
Ezekieli 14:1-3 |
| -Mafano amu mtima: | Marko 11:25; Mateyu 5:23 |
| -Mzimu wosakhululuka: | Miyambo 21:12; Yakobo 4:3 |
| -Kuzikonda, zolinga zolakwika: | Yakobo 4:2-3 |
| -Njala ulamuliro: | 1 Petro 3:7 |
| -Kukhala bwino ndi apabanja anu: | Luka 18:10-14 |
| -Kuziyelesa nokha: | Yakobo 1:6-7 |
| -Kusakhulupirira: | Yohane 15:7 |
| -Kusakhala mwa Khristu ndi mu Mawu Ake: | Yakobo 4:2-3 |
| -Kupempha kosiyana ndi chifuniro cha Mulungu: | Yohane 16:24 |
| -kupempha osagwiritsa ntchito dzina la Yesu: | Danieli 10:10-13; Aefeso 6:12 |
| -Zolepheretsa za ziwanda: | |
| -Kusayamba kusaka kaye Ufumu wa Mulungu: pamene mukuyamba kusaka Ufumu ndipamene mumalonjezedwa “zinthu zina”. | Mateyu 6:33 |
| -Pamene simukuziwa momwe mukuyenera kupempherera, pempheroo limalepheretsedwa. Ichi ndichifukwa chiri chofunikira kumulola Mzimu woyera kuti apemphere kudzera mwa inu. | Aroma 8:26 |

KUCHOTSA ZOLEPHERETSA PA KUPEMBEDZERA

Kumbukirani kuti kuzindikira kokha zolepheretsa sikukkwaniira, koma mukuyenera kumupempha Mulungu kuti akuthandizini kuzichotsa mu moyo wanu. Komanso mukumbukire kuti pemphero lomwe likuoneka kuti sirikuyankhidwa sizikutanthauza kuti muli zolepheretsa mu moyo wanu. Monga momwe takambira mu Chaputala 1, maynkho a mapephero atha kuchedwa kufika (Luka 19:7) kapena atha kukhala osiyana ndi zokhumba zathu (2 Akorinto 12:8-9).

NTHAWI IMENE SIMUKUYENERA KUPEMPHERA

Ndikofunikira kuphunzira m'mene tingadikirire ndi kupemphere pamaso pa Mulungu pofuna malangizo ndi chitsogozo chake. Ndikofunikiranso kuzindikira nthawi imene munthu sukuyenera kupemphera. Nthawi zina pemphero lanu la kupembedzera limapangitsa kuti Mulungu akuyitanene kuti mukagwire ntchito osati kuti mupemphere kwambiri.

Izi zikuonetseredwa pa nkhani ya ana a Israyeli pa madzi owawa ku Mira pamene amafunitsitsa madzi, koma sanakamwa kuchokera ku kasupe wowawa. Pamene Mose analirira kwa Ambuye popembedzera, Mulungu anamuonetsera zomwe akuyenera kuchita kuti madzi asiye kuwawa. Panalibe chifukwa chopitirabe kudikira pa Ambuye mu pemphero. Mose amayenera kuchita chimene Mulungu wamuuza kuti achite. Chomwechinso ndichooa ndi Yoswa amane amapembedzera m'malo mwa Israyeli atagonjetsedwa ndi Ai. Mulungu anaonetsera kuti panali tchimo akati pa anthu ndipo anamuuza Yoswa kuti...

Tauka, wagweranji pankhope pako cotere? ... Tauka, patula anthu... (Yoswa 7:10,12-13)

Iyi siyinali nthawi yopemphera koma inali nthawi yochita chimene Mulungu walankhula mu pemphero. Anthu ena amagwiritsa ntchito kupembedzera ngati njira yothawira kuchita zimene Mulungu wauza kuti achite. Kupembedzera kwa mphamvu kumabweretsa ntchito zakuya. Anthu ena apitirizabe kupemphera ingakhale Mulungu wawayankha koma sanasangalatsidwe ndi yankholo. Onani nkhani ya Balamu pa Numeri 22. Onani kwambiri mavesi 18-19. Balamu analibe kuthekera kopitanso pamaso pa Mulungu ndi pempho lomwelo chifukwa Mulungu anali atayankha kale (onani vesi 12).

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani vesi yotsogolera.

2. Lembani zolepheretsa za kupembedzera kochitachita zomwe zakambidwa mu chaputala ichi.

3. Kodi ndi nthawi iti imene simukuyenera kupembedera?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

CHAPUTALA 6

KUGWIRITSA NTCHITO PEMPHERO LA CHITSANZO POPEMBEDZERA

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kupereka chitsanzo cha pemphero la chitsanzo.
- X Kufotokoza chifukwa chimene pemphero la Ambuye liri pemphero lopembedzera.
- X Kunena pemphero lachitsanzo osaonera.
- X Kugwiritsa ntchito pemphero lachitsanzo popembedzera.

VESI YOTSOGOLERA:

**Atate wathu wa Kumwamba,
Dzina lanu liyeretsedwe.
Ufumu wanu udze.
Kufuna kwanu kucitidwe,
Monga Kumwamba comweco pansu pano.
Mutipatse ife lero cakudya cathu calero.
Ndipo mutikhulukire mangawa athu,
Monga ifenso takhulukira amangawa anthu.
Ndipo musatitengere kokatiyesa,
Koma mutipulumutse kwa woipayo. (Mateyu 6:9-13)**

CHIYAMBI

Pali mitundu iwiri ya “Pemphero la Ambuye” kapena “Pemphero lachitsanzo.” Ina yalembedwa pa Mateyu 6:9-13 ndipo ina pa Luka 11:2-4. Anthu ambiri ophunzira amagwirizana kuti kufanana kwa pakati pa mapempherowa kumapangisa kuti akhale pemphero imodzi.

Pa Mateyu pemphorori linaperekedwa linaperekedwa pamene Yesu amaphunzitsa Chiphunzitso cha Paphiri. Ndime ya mu boku la Luka linaperekedwa patapita zaka ziwiri ndi theka pamene ophunzira anabwera kwa Yesu ndikumufunsa kuti awaphunzitse m'mene angapempherere. Ophunzira amamuona Yesu m'mene akupemphera ndi kuona mphamvu imene imatsatira mapemphero Ake. Izi zinapangitsa kuti okhulupirira akhale ndi chikhumbokhumbo chofuna kudziwa kupemphera, ndipo anamufunsa Yesu. “Tiphunzitseni kupemphera.”

Yesu anayankha ndi mawu omwe amatchulidwa kuti “pemphero la Ambuye”:

**Cifukwa cace pempherani inu comweci
Atate wathu wa Kumwamba,
Dzina lanu liyeretsedwe.
Ufumu wanu udze.**

**Kufuna kwanu kucitidwe,
Monga Kumwamba comweco pansi pano.
Mutipatse ife lero cakudya cathu calero.
Ndipo mutikhululukire mangawa athu,
Monga ifenso takhululukira amangawa anthu.
Ndipo musatitengere kokatiyesa,
Koma mutipulumutse kwa woipayo. (Mateyu 6:9-13)**

PEMPHERO LA KUPEMBEDZERA

Pamene ophunzira anabwera kwa Yesu, anati “Tiphunzitseni ife kupemphera,” osati “Tiphunzitseni ife pemphero.” Yesa anawayankha pakugwiritsa njira imene aphunzitsi achi Yuda amakonda kugwiritsa ntchito. Aphunzitsi amakonda kutchula mitu wa choonadi, ndipo pansi pa mutu wina uliwonse amafotokoza ndondomeko yonse.

Mu pemphero lachitsanzoyi, Yesu anagwiritsa ntchito njira yomweyi yophunzitsira. Anapereka mitu ndi kufotokoza, “Cifukwa cace pempherani inu comweci.” “Cifukwa cace pempherani inu comweci” (*houtos oun* muchi Greek) kutanthauza kuti “kupemphera ngati uku.” Yesu sanawauze ophunzira ake kuti azibwereza mawu a pemphero, koma kupemphera “comweci.”

KUSANTHULA PEMPHERO

ATATE WATHU WA KUMWAMBA:

Mawu oti “Atate wathu” akusonyeza chifupi, koma mawu oti “wa Kumwamba” akuonetsa kutalika. Masalimo 139 akuonetsa, kuti Mulungu ali paliponse. Tikamapemphera kwa “Atate wathu wa Kumwamba,” sizikutsimikiza mtunda umene uli pakati pa ife ndi Atate, koma imatibweretsa ife kuchokera ku dziko la kuthupi ku dziko lamphamvu la uzimu. Tikamapemphera “Atate wathu wa Kumwamba,” timalumikizana kudzera mwa Khristu ndi Mulungu wamphamvu ndi chuma cha uzimu chomwe chitha kugwiritsidwa ntchito pa pemphero la kupembedzera.

DZINA LANU LIYERETSEDWE.

Pamene takhala mamembala a banja la Mulungu, Dzina la Atate wathu wa Kumwamba limapatsidwa kwa ife ngati momwe mwana wongotengedwa padziko lapansi amatengera dzina la Atate ake atsopano. Umwana wathu wa uzimu umatipasa kutekera koitana Mulungu “Atate” ndikulandira zolowa zonse zomwe zimagwirizana ndi Dzina Lake chifukwa ndife ana a Ufumu wa Atate.

Dzina la Mulungu sichidzindikiro chabe koma kuonetsero cha chikhaliidwe Chake ndi chivomerezo. Pamene tikuti “Dzina lanu liyeretsedwe” timalengedza umunthu, mphamvu ndi ulamuliro wa Mulungu. Pamene mukupempherera anthu ena, mutha kugwiritsa ntchito mayinawa popembedzera kwa Mulungu kuti agwire ntchito mu miyoyo yawo. Chitsanzo:

*“Ndikupempherera mkazi wanga, kuti inu mukhala Yehova-shalom kwa iye,
ndikupemphera kuti mukhala Yehova-jireh, opereka chosowa chirichonse mutsiku lino.*

*Yehova-nissi, ndikupemphera kuti mbendera yanu ikalamulira pa moyo wawo.
Ndikupemphera ngati Yehova-m'kaddesh muwayeretsa m'tsiku lalero... (etc.)”*

Mayina otsatirawa akufotokoza matanthauza amayina asanu ndi awiri a Mulungu:

DZINA	TANTHAUZO	CHITSANZO
Yehova-Jireh	Ambuye apereka	Genesis 22:14
Yehova-Nissi	Ambuye mbendera yanga	Eskodo 17:8-15
Yehova-Shalom	Ambuye Mtendere wathu	Oweruza 6:24
Yehova-Raah	Ambuye m'busa wanga	Masalimo 23:1
Yehova-Tsidkenu	Ambuye chilungamo chatu	Yeremiya 23:6
Yehova-Shammah	Ambuye ali pano	Ezekieli 48:35
Yehova-Rapha	Ambuye mchiritsi	Eskodo 15:26

UFUMU WANU UDZE:

Mu chigiriki, Chiheberi, ndi Chiaramu “Ufumu” wa Mulungu umatanthauza ufumu, ulamuliro, ndi zochita za ulamuliro wa Mulungu. Ndi kuonotsera chikwaridwe cha Mulungu.

Ulamuliro wa Mulungu utha kuodedwa ngati zochitachita za Mulungu pa dziko lonse lapansi; Mpingo wooneka wumene kudzera mwa iwo Ufumu umakudzidwa; ndi anthu amene Ufumu umapangidwa, ndi, okhulupirira onse obadwa mu Ufumu.

Nthawi ina mtsogolomu Ufumu wa Mulungu udzakhadzikitsidwa mu maonekedwe akuthupi. Ife sitikudzidwa nthawi yeniyeni ya izi (Machitidwe 1:7), koma malingana ndi Mawu a Mulungu izi zizachitika ndithu. “Maufumu onse a dziko lapansi” adzakhala katundu wa Mulungu, Ufumu woyipa wa Satana udzagonjetsedwa, ndipo Mfumu yathu idzalamulira ku nthawi zosatha (Chibvumbulutso 11:15).

Uthenga wa Ufumu uli womveka bwino mu Chipangano Chatsopano. Unakambidwa ka 49 mu Mateyu, 16 mu Marko, ndi 38 mu Luka. Yesu anayamba utumiki wake pakulengedza kuti kufika kwa Ufumu (Mateyu 4:17). Anamalidza utumiki wake pokamba zinthu za Ufumu (Machitidwe 1:3). Mu utumiki wake wonse anakamba za Ufumu. Nthawi zonse amalengeza kuti Akuyenera kulalikira uthenga wa Ufumu ku madera ena (Luka 4:43). Fanizo linalirironse la Yesu limakhuzana ndi Ufumu ndi moyo umatsata mfundo zake.

Yetsu anaonetsera kuti ife, ngati okhulupirira, tikuyenera kutsimikiza za Ufumu.

Koma muthange mwafuna Ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjedwa kwa inu. (Mateyu 6:33)

Vesi imeneyi ikuonetsera komwe tikuyenera kulunjika mapemphero, kulalika, kuphunzitsa, ndi makhalidwe athu. Zonse zikuyenera kulunjika ku Ufumu wa Mulungu. Pamene “tikuyamba kufuna Ufumu wa Mulungu,” zimatsimikiza mayankho a zinthu zina zimene zikutsatira mu pemphero lachitsanzo.

Kupemphera koti “Ufumu Wanu udze” ndikosiyana ndi pemphero lopemphera kuti Yesu abwerenso ndi kuzakhazikitsa Ufumu mu maonekedwe ake otsiriza. Tikapemphera kuti “Ufumu Wanu Udze,” timakhala kuti tikulengedza kuti Atete athu adziramulira mu miyoyo ya okhulupirira, osakhulupirira, ndi dziko lonse lapansi. Tikupempherera kuti Mulungu akavomeredwe ngati Mfumu ndikuti moyo pano padziko ukuyenera kulumuliridwa ndi malamulo ake.

Tikamalankhula mawu oti “Ufumu Wanu udze” timakhala kuti tikumupempha Mulungu kuti achotse chirichotse chotsutsana ndi Ufumu Wake, kuphatikidza mawu, makhalidwe, machitidwe azinthu, etc., mu miyoyo yathu ndi anthu ena.

KUFUNA KWANU KUCITIDWE MONGA KUMWAMBA COMWECO PANSI PANO:

Mu Chigiriki muli mawu awiri omwe amagriritidwa ntchito pokamba za “chifuniro” cha Mulungu. Mawu amodzi ndi “*boulema*”. Mawuwa amatanthauza chifuniro cha Mulungu cha umulungu dongosolo lomwe linakonzedweratu la chinachirichonse chomwe chomwe chimachitika pa dziko lonse. Mtundu wa “chifuniro” uwu umakwaniritsidwa kusatengera ndi zisankho zochitika ndi munthu. Ndi dongosolo Lake la dziko lonse ndi Mulungu kugwira ntchito padziko yokwaniritsa china chirichonse malingana ndi chifuniro cha umulungu Wake.

Mwa iye tinayesedwa colowa cace, popeza tinakonzekeratu monga mwa citsimikizo mtima ca iye wakucita zonse monga mwa uphungu wa cifuniro cace. (Aefeso 1:11)

Chifuniro cha Mulungu cha “*boulema*” sichimafuna kupezeka kwa munthu. Mu chifuniro cha Mulungu cha “*boulema*,” zotsatira zake ndizoti zinakonzedweratu pachiyambi. Chifuniro cha Mulungu cha “*boulema*” ndi Mawu Ake olembedwa ndipo ndizachiziwikire. Palibe chifukwa chosakasaka chifukwa chimenechi cha Mulungu chifukwa chimaonetseredwa mu Baibulo.

Mawu ena a chifuniro cha Mulungu ndi “*thelema*” ndipo chimatanthauza dongosolo la Mulungu pa munthu wina aliyense payekha payekha. Kuti Mulungu akakwaniritse chifuniro chake cha “*thelema*,” zimafunika m’gwirizano wa munthu. Anthu ali ndi mphamvu yosankha kuyenda kapena osayenda mu chifuniro cha Mulungu cha “*thelema*.” Mukamapemphera kuti “Kufuna kwanu ku chitidwe” pa moyo wanu kapena pa munthu wina, mumakhala kuti mukupembedzera chifuniro cha Mulungu cha “*thelema*” kuti chichitidw.

MUTIPATSE IFE LERO CAKUDYA CATHU CALERO:

Mu pemphero la chitsanzo, timayamba kufuna Ufumu pamene timalengeza kuti “Ufumu Wanu udze” pa nyengo ina ili yonse mu miyoyo yathu. Timazipereka mu chilungamo ku chifuniro cha Atete wa Kumwamba, pakulengedza “Kufuna kwanu ku chitidwe.” Pano ndiye titha

kumapemphera ndi chitsimikizo, “Mutipatse ife lero chakudya chatu chalero,” popempha kuti zosowa zathu zikwaniritsidwe zomwe zingatithandize ife kukwaniritsa chifuniro Chake ndi kukudza Ufumu Wake.

“Mutipatse” kumakhala kuvomereza kuti Mulungu ndiye gwero lathu. Mawu achigiriki omwe atanthauzira “chalero” mu pemphero la chitsanzo, sakupezeka penapaliponse mu Baibulo. Akutanthauza kuti “chakudya chofunikira, chokwanira kutsunga ndi kutilimbikitsa.” Kagwiritsidwe kaye ka ntchito mu pemphero lachitsanzo la Yesu zikutsimikiza kuti likuyenera kupempheredwa tsiku ndi tsiku.

Pemphero ndi la “chakudya” chomwe chikuonetsera kuti ndi chakudwa chaku uzimu ndi kuthupi komwe. Mawu oti “ife” akutanthauza kuti tikupembedzera “chakudya chatu chalero” cha anthu ena komanso ife eni ake.

NDIPO MUTIKHULULUKIRE MANGAWA ATHU, MONGA IFENSO TAKHULULUKIRA AMANGAWA ANTHU:

Tikuyenera kuphunzira kulandira ndi kupereka chikhulukiro anthu ena omwe atilakwira. Nthawi zambiri anthu timamulakwira Mulungu kudzera muzochima zathu. Mumathana nazo pomupempha Mulungu kuti akukhululukireni pamene mukunena, “Mutikhululukire mangawa athu.” Baibulo limalengeza:

Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi. Ngati tibvomereza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama iye, kuti atikhululukire macimo athu, ndi kutisambitsa kuticotsera cosalungama ciri conse. (1 Yohane 1:8-9)

Mukavomereza machimo anu omwe akudziwika Mulungu amakhululukira ingakhale machimo omwe sakudziwika ndi omwe mwavomereza, kukuyetsani ku kusalungama conse.

M'mbali yina yachiwiri imene kukhulukukira kukuyenera kuonetseredwa ndi kukhululukira anthu ena ku zolakwa zomwe atichirira zoziwika ndi zosaziwika. Zolakwa zoziwika ndi zimene munthu wina wakuchitirani. Zolakwa zosaziwika ndi zimene munthu wachitira bwanzi lanu kapena wapabanja panu ndipo mwazitenga kukhala kuti mwalakwiridwa ndi inu. Yesu anatiphunzitsa kuti tikuyenera kuthana ndi zolakwikazi pakupemphera kuti “Mutikhululukire mangawa athu, monga ifenso tawakhululukira amangawa athu.”

Nkhani ndiyoti, tisanayambe kufuna chikhulukiko kuchokera kwa Mulungu tikuyenera kuyamba kuwakhululukira amangawa athu. Yesu anaphunzitsa mfundoyi mu fanizo la wamangawo wopanda chifundo pa Mateyu 18:22-35. Nkhaniyi ikuonetsera kuti chikhulukiko cha Mulungu chimabwera pambuyo pa chikhulukiro cha anthu. Chikhulukiro cha anthu chimaonetsera chikhulukiro cha Mulungu, ndipo chikhulukiro cha Mulungu chimakhala choona pa ife pamene tiri okonzeka kukhululukira wina ndi nzake.

Yesu anafupikitsa choonadichi pamene analengedza:

Ndipo pamene muimirira ndi kupemphera, kholulukirani, ngati munthu wakulakwirani kanthu; kuti Atate wanunso ali Kumwamba akhulolukire inu zolakwa zanu. (Marko 11:25)

Satana ndi gwero la zolakwika mu banja lanu, pakati pa abwenzi, mu maubale azamalonda, ndi mu mpingo wanu. Baibulo limati “zokhumudwitsa zizabwera” (Mateyu 18:7). Kodi inu mudzathana nazo bwanji yengo ngati idzi zikadzadza? Kodi inu mazadzipembedzera mu pemphero kapena mudzangoziyankhula kudzera mu miseche?

NDIPO MUSATITENGERE KOKATIYESA, KOMA MUTIPULUMUTSE KWA WOIPAYO

Yesu anatiphunzitsa kupempera, “musatitengere kokatiyesa,” koma Yakobo ananena kuti Mulungu samuyetsa munthu:

Munthu poyesedwa, asanena, Ndiyesedwa ndi Mulungu; pakuti Mulungu sakhoza kuyesedwa ndi zoipa, ndipo iye mwini sayesa munthu. (Yakobo 1:13)

Kodi oyesa ndi ndani amene Yesu akufotokoza? Baibulo limationetsera kuti ndi Satana (Mateyu 4:3; 1 Atesalonika 3:5). Malembo kawirikawiri amatchenjeza za mayesero omwe amachokera kwa mdierekezi (Mateyu 4:1; 1 Akorinto 7:5; 1 Atesalonika 3:5). Baibulo limakamba kuti...

koma munthu ali yense ayesedwa pamene cilakolako cace ca iye mwini cimkokera, nicimnyenga. Pamenepo cilakolakoco citaima, cibala ucimo; ndipo ucimo, utakula msinkhu, ubala imfa. (Yakobo 1:14-15)

Satana ndi woyesa, koma ife timalowa m'mayeselo pamene ndilola zilakolako zathupi kutikoka. Zilakolako zimenezo zimabala tchimp, ndipo tchimo libala imfa. Kuukira kwina kwa Satana kumachokera ku zilakolako zoyipa zomwe zichokera mkati mwathu, pomwe mayesero ena machokera kunja kudzera mu zinthu zomwe tikumva, kuona, kukhudza, ndi kulawa. Posatengera gwero lake, Paulo Mtumwi anatitsimikizira kuti:

Sicinakugwerani inu ciyeso koma ca umunthu; koma Mulungu ali wokhulupirika, amene sadzalola inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza; koma pamodzi ndi ciyeso adzaikanso populumukirapo, kuti mudzakhoze kupirirako. (1 Akorinto 10:13)

Tikamapemphera kuti “Musatitengere kokatiyesa,” timakhala kuti tikumupempha Mulungu kuti atitetedzere ku zokometsa za uchimo. Ingakhale Yesu samatengeredwe kokayesedwa, koma anasungidwa mu izo (Ahebri 4:15). Paulo Mtumwi anatitsimikizira kuti:

Tidziwa kuti yense wobadwa kuokera mwa Mulungu sacimwa, koma iye wobadwa kuokera mwa Mulungu adzisunga yekha, ndipo woipayo samkhudza. (1 Yohane 5:18)

Pa Aefeso 6:10-18, Paulo Mtumwi anapereka uthenga wokhuza oyipayo ndi zida zauzimu zomwe zaoerekedwa ndi Mulungu pa chitetedzo chathu. Paulo ananenetsa kuti tichirimike mwa Ambuye, ndi m'kulimbika kwa mphamvu yache ndi kuchirimika pokana machenjerero a mdierekezi. (Aefeso 6:10,11,13).

Paulo ananenetsa kuti nkondo yomwe tikulimbana si nkondo yakuthupi ndipo zida zakuthupi sizingagwire ntchito. Nkhondo za uzimu zikuyenera kumenyedwa ndi zida zauzimu:

Mwa ici mudzitengere zida zonse za Mulungu, kuti mudzakhoza kuima citsutsire pofika tsiku loipa, ndipo, mutacita zonse, mudzacirimika.

Cifukwa cace cirimikani, mutadzimangira m'cuuno mwanu ndi coonadi, mutabvalanso capacifuwa ca cilungamo; ndipo mutadzibveka mapazi anu ndi makonedwe a Uthenga Wabwino wa mtendere;

koposa zonse mutadzitengeranso cikopa ca cikhulupiriro, cimene mudzakhoza kuzima naco mibvi yonse yoyaka moto ya woipayo.

Mutengenso cisoti ca cipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, ndilo Mau a Mulungu;

Mwa pemphero lonse ndi pembedzero mupemphere nthawi yonse mwa Mzimu, ndipo poezera pamenepo cicezerere ndi kupembedzera oyer mtima onse. (Aefeso 6:13-18)

Cholinga cha zida zonse za Mulungu kuti mukathe kuyimitsa mivi yonse ya Satana. Paulo akukulamulirani kuti “mudzitengere” zida izi za uzimu zomwe zikutanthauza kuti ndi udindo wanu woyenera womwe Mulungu wapereka. “kudzitengera” zikutanthauza kuti kutenga chinthu ndi kuchigwiritsa ntchito nokha. Umu ndi m’mememungachitire pamene mukupembedzera tsiku ndi tsiku:

Zida	Zolengeza Zoti Muchite	Lonjezano Loti Mulandire	Mzimu Wotsutanananu Woti Muumange
Kudzimangira m'chuuno mwanu ndi choonadi	Yesu, ndinu choonadi change	Yohane 14:6	Chinyengo
Chapachifuwa cha chilungamo	Yesu, Ndinu chilungamo	2 Akorinto 5:21	Kusalungama
Kuzibveka mapazi ndi makodzedwe a Uthenga Wabwino	Yesu, Ndinu chivomerezo change.	Afilipo 4:13	Ulesi
Chikopa cha chikhulupiriro	Yesu, Ndinu chikhulupiriro change.	Agalatiya 2:20	Kusakhulupira
Chisoti cha chipulumutso	Yesu, Ndinu chipulumutso change.	Ahebri 5:9	Maganizo oyipa

Lupanga la Mzimu Yesu,
(Mawu a Mulungu) Ndinu mawu anga a
moyo.

Yohane 1:14

Mabodza a Satana

CHIFUKWA WANU NDI UFUMU NDI MPHAMVU NDI ULEMERERO WA NTHAWI ZOSATHA:

Mawu oti “chifukwa” akuonetsa ulamuliro umene pemphero la chitsanzo lapemphedwera. Zimatanthauza kuti ufumu, mphamvu, ndi ulemerero ndi za Mulungu, titha kufunsa zotipatsa, malonjezano, ndi chitetedzo cha pempheroli. Tikafika pa gawo yomalidzayi ya pemphero lachitsanzo ndi kulengedza “Wanu ndi Ufumu,” timafipa pa mgwirizano wa china chirichonse chimene Mulungu wanena paza Ufumu Wake:

“Musaopa, kagulu ka nkhosa inu; cifukwa Atate wanu akonda kukupatsani Ufumu.” (Luka 12:32)

Mu Ufumu Wake, ngati ana ake, ndi Ufumu wathu ifenso. Ndi cholowa chomwe chaperekedwa ndi Atate.

Mawu omwe akuyimirira mphamvu ndi *dunamis*” omwe amatanthauza kuti “mphamvu yochitachita.” Pamene tikumalidza pemphero lathu ndi “wanu ndi mphamvu,” timakhala kuti tikuvomeraza mphamvu yochitachita ya Mulungu yomwe ikakwaniritse zopempha zathu zonse. Tikalengedza kuti “Wanu ndi maphamvu,” Mulungu amatibwenzera mawu a Yesu, “Ndakupatsani inu mphamvu pa mphamvu ya mdierekezi.” Idzi zimatsimikidza yankho kwa zinthu zonse zimene mwapembedzera mu pemphero lachitsanzo.

Kenako timalengedza kuti, “Wanu ndi ulemerero!” “Ulemerero” ndi mawu amene ali ndi matanthauzo ochulukana. Mawu ena amene amatanthauza ulemerero ndi: Ulemu, matamando, kukongola, mphamvu, kukwedzedwa, oyenera, kutchukitsa, ndi udindo. Yesu anati:

Ndipo ulemerero umene mwandipatsa Ine ndapatsa Iwo; kuti akhale amodzi, monga Ife tiri mmodzi. (Yohane 17:22)

Ulemerero umene Yesu analemekedzedwa nawo ndi Atate ndi mphatso kwa ife. Chomwe mukuyenera kuchita ndi kuwulandira. Mukuyenera kumakula kuchokera ku “ulemerero kupita kuulemerero” osati kugonjetsedwa kupita kugonjetsedwa. Inu mutha kukhumudwitsidwa ndi kumva kuti mulibe moyo mu uzimu, koma Mawu a Ambuye lero kwa inu ali...

Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwake kwafika, ndi ulemerero wa Yehova wakuturukira. Pakuti taona, mdima udzaphimba dziko lapansi, ndi mdima wa bii mitundu ya anthu; koma Yehova adzakuturukira, ndi ulemerero wace udzaoneka pa iwe. (Yesaya 60:1-2)

Ulemerero wa Mulungu umatsimikidza:

-Chuma cha Mulungu:
-Mphamvu:
-Chimwemwe:

Afilipi 4:19; Aefeso 3:16
Akolose 1:11
Yesaya 66:5; 1 Petro 1:8; 2 Mбири 16:10

-Mtendere:	Yesaya 60:1
-Kupuma:	Yesaya 11:10
-Chiyeretso:	Eskodo 29:43
-Mgwirizano ndi okhlupirira ena:	Yohane 17:22

Mawu awa akutanthauza chimene amanena... “nthawi zosatha” zomwe ziri kusatha, kukhala kopanda malire.” Pamene mukutseka pemphero lanu, inu mukupatsa Ufumu, mphamvu, ndi ulemerero kwa Atate wanu...*nthawi zonse*. Inu mukudzirumikidza nokha ndi mgwirizano wamuyaya ndi Atate anu chifukwa mukuvomereza inu mukutenga nawo gawu mu Ufumu, mphamvu, ndi ulemerero Wake.

AMENI:

Tikagwiritsa ntchito mawu oti “Ameni,” amasindikidza pemphero lathu ndi ulamuliro wamphamvu chifukwa “Ameni” ndi dzina limodzi la Khristu (Chibvumbulutso 3:14). Khristu amatchedwa “Ameni wa Mulungu,” chifukwa malonjezano one a Mulungu amakwaniritsidwa mwa Iye. Tikanena kuti “Ameni” zikutanthauza kuti tapemphera mapemphero onse mu dzina la Yesu.

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani maVesi otsogolera (pemphero la Ambuye.

2. Kodi zitsanzo ziwiri za pemphero la chitsanzo ziri pati mu Baibulo?

3. Kodi ndi chifukwa chiyani pemphero la Ambuye liri pemphero lopembedzera?

4. Kodi m ungagwiritse ntchito bwanji pemphero lachitsanzo popembedzera?

5. Kodi mungagwiritse ntchito bwanji mayina a Mulungu popembedzera anthu ena?

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Kupemphera malonjedzano a Mawu a Mulungu amatsimikidza mayankho ku mapemphero athu. Yambani kuwerenga Baibulo lanu ndipo chongani lonjezo lina lirilonse.

Yambani kugwiritsa ntchito malonjezanowa mukamapemphera. Mumapanga idzi popemphera lonjezalolo. Mwachitanzo umu ndi m'mene mungapempherere Masalimo 9:9-10:

“Ndikupempherera (dzina) kuti Inu mukhala pothawirapo pake m'nyengo za nsautso; Ndikupemphera kuti iye adzakhulupirira Inu; Pakuti, Inu Yehova, simunawasiya iwo akufuna Inu.”

Tsopano...inu yetserani. Pedzani laonjeza kuchokera mu Baibulo ndipo ilembeni pansipo mu maonekedwe a pemphero:

CHAPUTALA 7

KUPEMBEDZERA CHITSITSIMUTSO

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kutanthauza chitsitsimutso.
- X Kufotokoza momwe tingakonzekerere chitsitsimutso.
- X Kudzindikira pamene chitsitsimutso chikufunika.
- X Kudzindikira zizindikiro za chikhalidwe chobwerera m'buyo.
- X Kulemba mwachidule mfundo za m'Baibulo za chitsitsimutso.
- X Kudzindikira zolepheretsa za chitsitsimutso.
- X Kufotokoza m'mene mungagwiritsire ntchito “dongosolo la Mulungu ya chitsitsimutso” popembedzera chitsitsimutso.

VESI YOTSEGOLERA:

Ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhululukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao. (2 Mbiri 7:14)

CHIYAMBI

Ntchito imodzo yofunikira mwa ntchito za kupembedzera ndi kupempherera chitsitsimutso. Mu chaputala ichi muphunzira tanthauzo la chitsitsimutso, m'mene mungakonzekere, ndi m'mene mungadzindikire pamene chitsitsimutso chikufunikira. Muphunziratso m'mene mungadzindikire zolepheretsa zimene zimalepheretsa chitsitsimutso ndi m'mene mungapembedzerere.

TANTHAUZO LA CHITSITSIMUTSO

Poyamba, tiwone chimene chitsitsimutso sichiri. Chitsitsimutso si maimvaimva okha chabe. Anthu amavomereza chitsitsimutso kutengera ndi momwe akumvera, koma maimvaimva ndi mbali ya chitsitsimutso, iwo si chitsitsimutso. Chitsitsimutso chenicheni chimakhudza munthu yense, koma, kuphatikizanso zomvaimva. Chidziwitso cha mfundo sichisuntha anthu. Chiwerengero cha anthu omwe akufa chifukwa cha mowa sichisuntha munthu wolezera. Chiwerengero chochuluka cha upandu sichisuntha zigawenga. Mphamvu yotsutsa ya Mzimu Woyera ikuyenera kukhudza uzimu ndi maimvaimva kuti munthu akasinthe.

Chitsitsimutso si nyimbo zomveka patala ndi ulaliki wa “moto waku gehena.” Si kampeni kuti mamembala atsopano alowe mu mpingo. Kukula kwa Mpingo ndi zotsatira za chitsitsimutso, koma si chitsitsimutso. Chitsitsimutso si uvangeli. Uvangeli ndi kulengedza za Uthenga Wabwino. Chitsitsimutso chimayamba pa uvangeli, chifukwa akufa akakhulupirira “amatsitsimuka,” zotsatira za uvangeli. Pomalidza, chitsitsimutso si misonkhano yokumana pafupi pafupi...pokhapokha misonkhanoyo ikhale kuti yakhudzina ndi kuyenda kwa Mulungu.

Chitsitsimutso ndi...

“Ntchito za umulungu zodabwitsa za Mulungu zodzera ndi m’ malo mwa anthu omwe aphunzira ndi agwirotsa ntchito mfundo za Mawu a Mulungu a rhama okhudzana ndi chitsitsimutso.”

Chitsitsimutso ndi cha umulungu, zomwe zikuti sichingapangidwe ndi munthu. Ndi chodabwitsa, chifukwa ndi ntchito yapaderadera ya Mulungu. Chitsitsimutso chimagwira ntchito pakati pa anthu ndi m’ malo mwawo. Pofuna kukonzekera za chitsitsimutso, tikuyenera kugwiritsa ntchito mfundo zimene zabvumbulutsitsa mu Mawu a Mulungu zokhudza chitsitsimutso. China chirichonse chimene Baibulo limaphunzitsa zokhudza chitsitsimutso ndi “rhema” kapena Mawu a Mulungu olankhulidwa. Titha kunenanso kuti chitsitsimutso ndi:

-Kudzuka, kubwedzeretsedwa kwa anthu a Mulungu, kupereka mphamvu ku znthu zomwe zasalira.

-Kubwerera ku kutsitsimuka kapena ku moyo. Chithu chomwe chimatsitsimuka chimakhala chochitachita.

-Nthawi yotsitsimutsa kuchokera ku kupezeka kwa Mulungu. (Machitidwe 3:19)

KUKONZEKERA CHITSITSIMUTSO

Titha kufananiza kukonzekera kwa chitsitsimutso ndi ntchito ya m’ mlimi. Mlimi atha kupempherera zokolola zabwino, koma ngati sakonzeketsa munda wake, kubzala mbewu, kuthirira mbewu, sangakolore.

Chimodzimodzi opusa ndi mlimi yemwe amaganiza kuti chifukwa wagwira m’ bali yake ndiye kuti zokolola ndizotsimikidza. Zimatengera Mulungu kubweresa mvula, kuwala kwa nzuwa, ndi nyengo yabwino kuti mbewu zikhwime. Mlimi amagwira ntchito mogwirizana ndi mfundo za kubzala ndi kukolola, nthawi ya kubwala ndi yokolola yawonetseredwa mu Mawu a Mulungu. Mulungu ndi wachifundo, chifukwa mvula, nzuwa, ndi nyengo ywbwino zimachokera kwa Iye.

Kufananizira komweku kutha kugwiritsidwa ntchito ndi chitsitsimutso. Ndi kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu, koma “kukolola” chitsitsimutso, tikuyenera kukonzekera pakutsata mfundo za chitsitsimutso zomwe zawonetseredwa mu Mawu a Mulungu. Chitsitsimutso ndi kugwirizana kwa kuyenda kwa Mzimu Woyera ndi kuvomereza kwa anthu a Muungu.

NTHAWI IMENE CHITSITSIMUTSO CHIKUFUNIKA

Inde chitsitsimutso chimafunika nthawi zonse, koma chimafunikira kwambiri pamene kubwerera m’ buyo kukuonekera. Kutu mudzindikire kubwerera m’ buyo, onani chitsanzo cha Israyeli. Yeremiya anatchula mavuto a Israyeli “kubwerera m’ buyo” (Yeremiya 1:3-4). Baibulo limati:

Wobwerera m’mbuyo m’mtima adzakhuta njira zace; Koma munthu wabwino adzakhuta za mwa iye yekha. (Miyambi 14:14)

Pitani ku Yeremiya chaputala 2. Inu mupeza kuti Israyeli anali..

- Kutsimikiza kuti Mulungu sanali wofunikira ngati monga analiri poyamba: 2:5
- Kuyiwala zinthu zazikulu zimene Mulungu anawachitira poyamba: 2:6-7
- Ingakhale akulu akulu a chipembedzo analowa nawo mugulu la obwerera m'buyo. Ansembe analephera kufunsa, "Ambuye ali kuti?": 2:8
- Mulungu anachoka pamaso pawo, anapita ku zinthu zina... mafano: 2:11-12; 27-28
- Anayiwala chisime chenicheni cha madzi a uzimu ndipo anayamba kumapita ku zisime zomwe sizingathe kusunga madzi: 2:13
- Anayamba kuowerera mu uzimu: 2:19
- Analowa mu chiyero chozipasa okha: 2:22-23
- Anazilungamisa okha: 3:11
- Anatengera ena mu chivundi chawo: 2:33-34

Kubwerera m'buyo ndi uchimo omuchosa Mulungu ndi kudzadza moyo wanu ndi inu nokha. Kumafotokozeredza kuti nkumba kubwerera ku matope ndi galu kubwerera ku masanzi ake. (2 Petro 2:21-22)

ZIZINDIKIRO ZA CHIKHALIDWE CHOBWERERA M'BUYO

1. Pamene pemphero lasiya kukhala mbali yofunikira pa moyo wanu.
2. Pamene njala yofuna kudziwa choonadi cha m'Baibulo yatha ndipo muli okhutitsidwa ndi chidziwitso chomwe muli nacho. Izi sizikutanthauza kuti obwerera m'buyo sawerenga Baibulo. Ambiri a iwo ali ndi chikhalidwe chongotsatira malamulo chabe, koma akamawerenga mawu chidziwitso chomwe akupeza chimatengedwa ngati mbiri chabe ndipo sichigwira ntchito pa moyo wawo
3. Akaganizira za zinthu za muyaya sizikhalanso zopinduritsa kwa iwo.
4. Pamene zinthu zamasewero ndi zamsangulutso zikhala zoyamba pamoyo wanu.
5. Pamene mungachite tchimo lopanda kumva kutsutsika.
6. Pamene chikhumbokhumbo cha chiyero cha Khristu sichiritso chofunikira.
7. Pamene kuphwanya maubale sizimakukhuzani.
8. Pamene zilakolako za thupi zikulamulira moyo wanu: kumvera nyimbo kapena makanema omwe siali za umulungu.
9. Pamene mwataya mphamvu zanu za uzimu, ndipo simukuzindikira ichi.

ZOLEPHERETSA ZA CHITSITSIMUTSO

Izi ndi zinthu zina zimene zimalepheretsa kuyenda kwa mphamvu ya Mulungu mu mpingo:

ZOLEPHERETSA ZA UTSOGOLERI:

Aziraliki omwe salalikira ndi kuphunzitsa Mawu a Mulungu mu phamvu amalepheretsa chitsitsimutso. Iwo omwe alibe nthawi yapemphero, nthawo yowerenga Baibulo, opanda kuwonetsera kwa mphamvu amalepheretsa chitsitsimutso. Iwo omwe amalamuliro mpingo wawo ndi kudzimitsa Mzimu wa Mulungu amalepheretsatso kuyenda kwa Mulungu.

Adzitsogoleri omwe sasamala za nkhoa amalepheretsa chitsitsimutso. Samatsogolera nkhoa ku msipu obiriwira ndi kumadzi odikha ofunikira kuti awatsitsimutse. Adzitsogoleri omwe ataya kukhudzidwa mtima pa dziko lokufa amalepheretsa chitsitsimutso. Ambiri samazindikira udindo wawo wokhala atsogoleri mu chitsitsimutso (Yoweli 2:15-18)

ZOLEPHERETSA ZA MPINGO WONSE:

Mu mpingo wa anthu a Mulungu mutha kukhalanso zolepheretsa chitsitsimutso. Chikondi cha miyambo ya mpingo yomwe yimalepheretsa chitsitsimutso. Chitsitsimutso ndi kusintha zofanana. Mulungu ndi wadongosolo ndi wodalirika, komanso ali amapanga zinthu zatsopano ndi zofunikira. Iye sanunga zikhalidwe za anthu. Ngati mpingo ungamayendetsedwe malingani ndi zinkhalidwe za anthu, uyendetsedwa opanda mphamvu ndi kupezeka kwa Mulungu.

Mipingo yambiri imakonda chilungamo chonthoza. Samafuna kuti alalidwe za uchimo ndi chiweruzo. Chilungamo cha chitsitsimutso nthawi zonse sichithoza. Chikondi chapa anthu ena chimalepheretsa chitsitsimutso. Mipingo ina imakhudzidwa kambiri ndi kuti “kodi anthu azaganja zotani” kusiyanana ndi zimene Mulungu akuganiza.

ZOLEPHERETSA ZINA:

Pali zolepheretsa zina zimene zitha kupezeka mu utsogoleri ndi mu mpingo. Zolakwa zimalepheretsa chitsitsimutso, kaya zipezeka mwa munthu pa gome kapena ayi:

Taonani, mkono wa Yehova sufupika, kuti sungathe kupulumutsa; khutu lace siliri logontha, kuti silingamve (Kufuna kwathu kwa chitsitsimutso)...

koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo macimo anu abisa nkhope yace kwa inu, kuti Iye sakumva. (Yesaya 59:1-2)

Wobisa macimo ace sadzaona mwai; Koma wakuwabvomereza, nawasiya adzacidwa cifundo. (Miyambi 28:13)

Makhalidwe omanena kuti “ano ndi masiku otsiriza ndipo tikuyenera kuyembekedzera zinthu zipitirira kuipitsitsa” kumalepheretsa chitsitsimutso. Kusaonsa chidi ku pemphero ndi Mawu, kukala kuzichepesa, ndi kukana kufuna Ambuye kumalepheretsa chitsitsimutso. Kumuletsa Mulungu kumalepheretsa kuyenda kwake pakati pathu:

**Pakuti anabwerera m'mbuyo, nayesa Mulungu, Nacepsa Woyerayo wa Israyeli.
(Masalmo 78:41)**

**Ndipo Iye, cifukwa ca kusakhulupirira kwao, sanacita kumeneko zamphamvu
zambiri. (Mateyu 13:58)**

DONGOSOLO LA MULUNGU LA CHITSITSIMUTSO

Zolepheretsa zina ziri zonse zomwe takambirana zitha kuthetsedwa kudzera kupembedzera chifukwa chitsitsimutso chimabwera povomereza kuti tipemphere. Umu ndi m'mene mungapempherere chitsitsimutso:

Ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhulukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao. (2 Mbiri 7:14)

Mfundo zambiri za chitsitsimutso zakambidwa mu vesiyi. Poyamba, Mulungu akayankhula kwa anthu Ake (“ndipo anthu anga”). Akukamba ndi ochimwa, dziko, kapena wina aliyense. Mulungu akulankhula ndi anthu ake omwe “ochedwa dzina langa.” Izi ndi zomwe anthu a Mulungu akuyenera kuchita kuti akumane ndi chitsitsimutso

1. “AKAZICHEPETA”:

Kuzichepetsa nokha ndikuzibwerensa nokha pansu pa Mulungu (werengani Levitiko 26:40-41). Kuzichepetsaku kukuphatikidza kuzichepetsa pamaso pa Mulungu (2 Mbiri 34:1-13); Mawu Ake (2 Mbiri 32:14-28); ndi anthu Ake (2 Mbiri 34:29-33).

2. “NAKAPEMPHERA”:

Mukuyenera kupemphera mapemphero achindunji a (1) kufuna Mulungu ndi (2) kutembenuka kuleka njira zoipa. Nthawi zambiri “sitirandira” chifukwa “sitipempha” kapena timapempha ndizolinga zolakwika. Tikuyenera kumupempha Mulungu kuti atitsitsimutse ndi kupemphera mapemphero achindunji a kuvomereza ndi kulapa pokonzekeretsa mitima yathu pa kuyenda kwa Mzmu Wake.

3. “NAFUNA NKHOPE YANGA”:

Chiganizo choti “kufuna Mulungu” chagwiritsidwa ntchito mu ndime zotsatirazi za Chipangano Chakale:

Eskodo 33:7; Deuteronomo 4:29; Ezara 8:22; 2 Samueli 12:16; 21:1; 1 Mbiri 16:10-11; 2 Mbiri 7:14; 11:16; 15:4; 20:4; Maslimo 105:3-4; 24:6; 27:8; 40:17; 69:7; 70:5; Miyambo 28:5; Yesaya 51:1; Yereimiya 29:13; 50:4; Hoseya 3:5; 5:6-7,15; 7:10; Danieli9:3; Zefaniya 1:6; Zakariya 8:21; Malaki 3:1.

4. “NAKATEMBUNUKA KULEKA NJIRA ZAO ZOIPA”:

Pemphero ndi kufuna Muungu sizokwanira mwa izo zokha. Zikuyenra kuperekedzedwa ndi kulapa kuonadi mtima kumene kuli kusintha kopita. Mukuyenera kutembenuka naeka njira zanu

zoipa. Mpingo unayamba ndi muyitano wa kulapa (Machitidwe 2). Muyitano womaliza mu buku la Chibvumbulutso ndi kulapa (Chibvumbulutso 22:16).

Kulapa ndi mpatso yochokera kwa Mulungu yimene imakupangitsani inu kusintha njira zanu za moyo (Machitidwe 5:29-31; 11:15-18; 2 Timoteo 2:22-26). Anthu onse akulamulidwa kuti alape (Machitidwe 17:30). Ndichifuniro cha Mulungu kuti anthu onse alape (2 Petro 3:9) ndipo Mulungu amagwira ntchito mwa chisomo kuti abweretse anthu ku kulapa (Aroma 2:4). Popanda kulapa inu muzaonongedwa (Luka 13:3,5). Yesu analamulira kuti kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo kulalikidwe mu dzina Lake ku mitundu yonse (Luka 24:47).

MWACHIDULE:

Izi ndi zimene mukuyenera kuchita pokonzekera chitsitsimutso:

- Zichepeseni
- Pemphepani
- Funani nkhope Yake
- Katembenukeni ndikuleka njira zoipa

Izi ndi zomwe Mulungu angachite:

- | | |
|-------------------------------|---------------|
| -“AZAMVERA m’Mwamba”: | Yankho |
| -“KUKHULULUKIRA choipa chao”: | Kuyanjanitsa |
| -“KUCHIRITSA dziko lawo”: | Kubwenzeretsa |

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera

2. Tanthauzani chitsitsimutso.

3. Kodi tingakonzekere bwanji chitsitsimutso?

4. Kodi chitsitsimutso chikufunika nthawi zANJI?

5. Lembani mwachidule zizindikiro zina chikhalidwe chobwerera m'buyo.

6. Kulemba mfundo za m'Baibulo za chitsitsimutso zomwe zaperekedwa mu chaputala ichi.

7. Kufotokoza m'mene mungagwiritsire ntchito “dongosolo la Mulungu ya chitsitsimutso” popembedzera chitsitsimutso.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Zitsanzo chitsitsimutso cha Chipangano Chakale zaperekedwa kuti muonjezere kuphunzira.

CHITSITSIMUTSO MU NTHAWI YA YAKOBO:	Genesis 35:1-5
CHITSITSIMUTSO MU NTHAWI YA MOSE:	Eskodo 32:1-35; 33:1-23; machaputala 34-35
CHITSITSIMUTSO MU NTHAWI YA SAMUELI:	1 Samueli 7:1-17
CHITSITSIMUTSO MU NTHAWI YA ELIYA:	1 Mafumu 17-18
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA ASA:	2 Mbiri 14-15; 1 Mafumu 15:9-24
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA JEHOSAFATI:	2 Mbiri 20
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA HEZEKIYA:	2 Mbiri 29:1-36; 30:1-27; 31:1-21
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA YOSIYA:	2 Mbiri 34:1-33; 35:1-19
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA ZERUBABELO:	Hagai 1; Zekaliya 1:1-6
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA SOLOMONI:	2 Mbiri 6-7
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA YONA:	Buku la Yona
CHITSITSIMUTSO MU NTAHWI YA NEHEMIYA:	Nehemiya 8-10

CHAPUTALA 8

KUYAMBA NDI KUPITA CHITSOGOLO

ZOLINGA

Pomaliza pa chaputalachi mukuyenera kukwanitsa izi:

- X Kukonza ndondomeko yakapempheredwe
- X Kupanga ndondomeko yakapempheredwe
- X Kupembedzera mayiko ena
- X Kudzindikira zovuta zomwe zikuyenera kugonjetsedwa
- X Kudzipereka nokha ku utumiki wa kupembedzera.

VESI YOTSOGOLERA:

Koma iwe popemphera, Iowa m'cipinda cako, nutseke citseko cako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe. (Mateyu 6:6)

CHIYAMBI

Pophunzira pemphero la kupembedzera taphunzira chomwe iri, chuma cha uzimu chomwe chaperekedwa kuti chitithandidzire kuti tirichite, ndi momwe tingapempherere. Komanso taona pemphero lachitsanzo, Ambuye Yesu Khristu, komanso kuphunzira kuzindikira ndikuthana ndi zolepheretsa pemphero lochitachita. Chaputala chomalizachi chikupereka maganizo a momwe mungayambire ndi kupita chitsogolo ndi utumiki wa pemphero lopembedzera.

KUPANGA DONGOSOLO LOPEMPHERA

Ngati mukufuna kukhala opemphedzera ochitachita mukuyenera kukhala ndi nthawi yopemphera. Njira imodzi yopangira izi mukuyenera kukhala ndi ndondomeko yomwe mungamapempherere panokha ndi anthu ena. Chipangano Chatsopano chikuonetsera ndondomeko yakapempheredwe:

PEMPHERO LA PANOKHA:

Pemphero likuyenera kuchitipa mwapanokha:

Koma iwe popemphera, Iowa m'cipinda cako, nutseke citseko cako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe. (Mateyu 6:6)

Ikani nthawi padera tsiku lina lirironse yopemphera, makamaka mam'mawa a tsiku musanayambe kugwira ntchito zanu za tsiku ndi tsiku. Ngati simungakwanise “mam'mawa” pezani nthawi ina yomwe iri yabwino kwa inu. Iyi ndi nthawi yomwe mungamachite utumiki wanu wa unsembe woyima pamaso pa Mulungu ndi matamando ndi malambiridwe ndi pakati pa

Mulungu ndi munthu ndi zopempha ndi kupembedzera. Musanayambe kupembedzera muzikhala ndi nthawi yolapa ndi kumupempha Mulungu kuti akuyeretseni ku machimo onse. Kulapa ndi kofunikira pa kupembedza kochitachita.

ANTHU AWIRI KUPEMPHERA PAMODZI:

Ndiponso ndinena kwa inu kuti ngati awiri ainu abvomerezana pansu pano cinthu ciri conse akacipempha, Atate wanga wa Kumwamba adzawacitira. (Mateyu 18:19)

Pezani bwenzi loti muzitha kupembedzera naye limodzi nthawi ndi nthawi. Ngati muli okwatira mutha kusakha yemwe mwakatirana naye. Ngati muli ndi munthu yemwe mumapempha naye limodzi atha kumakulimbikitsani pamene inu mwafooka.

GULU LALING'ONO:

Gulu laling'ono limakhala ndi anthu opitirira awiri ogwirizana namapembedzera. Pali mphamvu yayikulu pomwe anthu awiri kapena atatu abwera pamodzi ndicholinga chimenechi.

Pakuti kumene kuli awiri kapena atatu asonkhanira m'dzina langa, ndiri komweko pakati pao. (Mateyu 18:20)

Munthu kufuna kumakuma sabata lina lirironse ngati gulu laling'ono la abwenzu, ogwira ntchito limodzi, kapena achibale.

PEMPHERO LA MPINGO WONSE:

Mpingo wonse ukuyeneranso kubwera pamodzi namapembedzera:

Iwo onse analikukangalika m'kupempha, pamodzi ndi akazi... (Macitidwe 1:14)

Machitidwe 12:5 akuonetsera kuti mpingo unapempherera Petro kosalekeza pamene iye anali ku ndende. Ngati muli abusa ndi udindo wanu kukonsa ndongosolo la nthawi ya mapemphero a mpingo wonse.

KUPANGA NDONDOMEKO YAKAPEMPHEREDWE

Ndizofunikira kupanga ndondomeko yakapempheredwe kuti ikutsogolereni m'mene mungapempherere. Gwiritsani ntchito kope lomwe mungalembemo magawo ngati awa:

-Dera ndi dziko lomwe mumakhala: Pedzani mapu a dera lanu ndi dziko lanu omwe mukuyenera kuti mudziwapempherera. Pedzani mayina a adzitsogoleri andale ndi chipembedzo ndikumawapempherera potchula mayina awo.

-Lembani zosowa za banja lanu, abwenzu anu, ndi anthu ena ndipo muzidzipembedzera tsiku ndi tsiku. Lembani mapemphero omwe ayankhidwa kuti azikulimbikitsani mtima.

-Mpingo wanu: Pazani mayina a mtsogoleri wina aliyense wa mpingo wanu ndikumawapempherera tsiku ndi tsiku. Pemphererani membala wina aliyense wa mpingo wanu potchula dzina lake.

-Utumiki wanu: Pemphererani utumiki wainu mwini. Ngati muli m'busa, pemphererani munthu winaaliyense wa mumpingo wanu potchula dzina lake. Ngati muli kholo, pemphererai ana anu (amene ali gawo la utumiki wanu). Ngati muli mvangeli, pempherani kuti makomo otumikira Uthenga Wabwino atseguke.

-Kupembedzera mayiko ena: Ikani gawo lopembedzera mayiko a dziko lonse lapansi ndi kukula kwa Ufumu wa Mulungu. Poti utumiki wa Harvestime International umalunjika ku utumiki wolalikira dziko lonse, tikufuna kuti tilumikize mautumiki athu onse pamodzi kudzera mupemphero. Chifukwa cha ichi, tapereka malangizo otsatirawa a utumiki wopembedzera mayiko ena.

KUPEMBEDZERA MAYIKO ENA

Awa ndi malangizo apaderadera a utumiki wopembedzera mayiko ena omwe atha kugwiritsidwa ntchito ndi munthu modzi, pa gulu kapena ndi mpingo wonse:

LEMEKEZANI MULUNGU: (mphindi 10)

Timalowa zipata za Mulungu ndi chiyamko ndi chiremekezo: Masalimo 10:4

KUPEMBEDZERA DZIKO LONSE LAPANSI: (mphindi 10)

Musanatyambe kupembedzera, pempharani pemphero lolapa machimo. Kenako pemphererani dziko lapansi kuti...

-Njala yatsopano wa uzimu padziko lonse.

-Mulungu kuti adzutse mphamvu ya dziko lonse ya utumiki wopembedzera mayiko ena.

-Kukula kwa Mpingo pa dziko lonse lapansi.

-Mulungu adzutse “ogwira ntchito m'munda.”

-Mgwirizana ndi kumvana kwa mipingo ndi mautumiki omwe alipo kale.

-Chitsitsimutso cha change ndi chifundo pofuna kuwina miyoyoyotayika.

-Kagwiritsidwe kanzeru ka chuma ndi okhulupirira pofuna kufaltsa Uthenga Wabwino. Mphempheni Mulungu kuti apereke chuma chofunikira ndi kudzutsa apene ali okhumba ndi kuthekera kothandiza utumiki.

-kutsekula makomo pofuna kufalitsa Uthenga Wabwino (Aefeso 6:19)

-Mayiko otsekeka kuti akatsegulidwe (2 Atesalonika 3:1).

-Kulandira kwa iwo omwe akumva Uthenga Wabwino (Aroma 15:30-31).

-Zinthu zimene zikukhuza kufaritsa Uthenga Wabwino.

-Kuti mitima ya boma ndi adzitsogoleri a ndale ikhale yolandira ntchito ya utumiki andi uvangeli.

- Ogwira ntchito omwe akubzala mipingo ndi mautumiki.
- Okhulupirira omwe amangidwa kapena omwe akuvutka chifukwa cha kudzipereka kwawo ku Kridu kapena chifukwa cha utumiki.
- Ntchito ya umasulira Baibulo pa dziko lonse lapansi.
- Malo ophunzitsira athu utumiki pa dziko lonse lapansi.
- Kuyanda kwa Mulungu pa achinyamata. Ndi adzitsogoleri a m'tsogolo a Mpingo.
- Chitetedzo kwa anthu ogwira ntchito. Mangani zichitochito za Satana zomwe zikudza motsutsana ndi okhulupirira. Pempherani kumasulidwa kwa iwo omwe amatsutsa Uthenga Wabwino (Aroma 15:30-31; 2 Atesalonica 3:2).
- Omwe amagwira ntchito malo mu mayiko osiyanasiyana ndicholinga chofalitsa Uthenga Wabwino.

KUPEMBEDZERA DERA LIMODZI LA DZIKO LAPANSI: (mphindi 10)

Gwiritsani ntchito mapu a dziko lapansi popempherera mayiko osiyanasiyana. Izi ndi zinthu zomwe mungamapembedz

- Mipingo ya m'dzikolo.
- Omwe akugwira ntchito ya uzimu mu zikolo. Iwo omwe akubzala mipingo.
- Okhulupirira a m'dzikoli.
- Anthu omwe sanafikiridwe ndi Uthenga Wabwino.
- Kumanga mphamvu za Satana zomwe zikugwira ntchito mu dzikolo; mphamvu zomwe zingabwere motsutsana ndi kufaritsidwa kwa Uthenga Wabwino kapena kutseka dziko kuti lisalandire Uthenga Wabwino.
- Mu dera lina lirironse muli zigawo asanu ndi awiri zomwe zimaonetsera tsogolo la dzikolo. Izi ndi mabanja, mpingo, maphunziro, luso ndi zosangalatsa, ofalisa uthenga, boma, ndi zamalonda. Pembedzerani magawo onse.

KUPEMBEDZERA UTUMIKI: (mphindi 10)

Pamene mukulumikizana ndi utumiki womwe ukufalitsa Uthenga Wabwino muzakhala ozindikira zosowa zawo zomwe mukuyenera kupembedzera. Lumikidzanani nawo kuti azikutumizirani zinthu zopembedzera.

KUPEMBEDZERA ANTHU AMENE SANAFIKIRIDWE: (mphindi 10)

Mitundu isanu ikuluikulu ya anthu yomwe sinafikiridwe ndi Abuda, Hindu, anthu achikhalidwe chamakolo, Asilamu, ndi Machina.

- Pemphererani njala ya uzimu pa magulu awa.
- Pemphererani ogwira ntchito kuti akafalitse Uthenga Wabwino kai wo.

- Pempherarani kubvumbulutsidwa kwa ndondomeko za bwino zofikira mtundu wina uliwonse pawokha pawokha.
- Pempherarani iwo omwe ayamba kale kufikira anthu amenewa.

PEMPHERO LA NOKHA: (mphindi 10)

Lingalirani zosawa zano poyerekezera ndi zosowa za dziko lonse. Kodi zosawa zanu zikugwirizana bwanji ndi zolinga za Mulungu pa dziko lonse ndi mbali yanu mu zimenezi? Nkhawa zanu nthawi zina zimagwirizana ndi zolinga za Mulungu pa dziko lonse. Funani Mulungu kuti akuonnetseremi njira zomwe mungakwaniritsire mbali yanu pa ntchito yofikira mayiko a dziko lapansi ndi Uthenga Wabwino wa ufumu. Kodi inu mungazikhozekeretse bwanji? Kodi mungayambe bwanji? Kodi mungapereke bwanji nthawi yanu ndi chuma chanu chifukwa cha utumiki?

ZOVUTA ZOMWE ZIKUYENERA KUGONJETSEDWA

Wina alayense amene anapempherako mochitachita anakumanako ndi mavuto omwe amayenera kuwagonjetsa. Kugonjetsa zophinjazi ndi mbali ya kupembedze:

“Kodi ndi ndani yemwe amakupasana chirakolako? Kozi amakupatsani kuti chisakwaniritsidwe? Izi ndi zosatheka. Amayikiza mwa inu chirakochako cha chinachake ndi cholinga chokupasani chinthu chimenecho; Azakupasani inu chimenecho gati mungapemphe mu njira yoyenerera...ndipo amakuthandizani inu kupempha kwake.” – Jean-Nicholas Grou

CHIYAMBI CHA MATHERO

Tafika kumathero kwa phunziro la kupembedzera. Muchilungamo chake, komano, simathero koma chiyambi. Mupatsidwa chomu chofunikira kwambiri chomwe chiri chopezeka pa Thupi la Khristu...chomwe chiri kupembedzera. Kudzera kupembedzera, mutha kufikwa kwina kulikonse mu uzimu. pemphero lano lina kufikira kumayiko omwe sanafikiriddwendi Uthenga Wabwino. Mutha kusintha tsogolo la munthu payekha payekha ndi dziko lonse. Mutha kupulumutsa miyoyo yotayika ya amuna ndi akazi, anyamata ndi asikana.

Mwalowa mu ubale ndi Mulungu kudzera mu kupembedzera. Mutha kupembera molimba mtima podziwa kuti:

Yehova wa makamu walumbira, nati, Ndithu monga ndaganiza, coteru cidzacididwa; ndipo monga ndapanga uphungu, coteru cidzakhala. (Yesaya 14:24)

Umenewu ndi uphungu wopangira dziko lonse; ndipo ili ndi dzanja lotambasulidwa pa amitundu onse.

Pakuti Yehova wa makamu wapanga uphungu, ndani adzauleketsa? ndi dzanja lace latambasulidwa, ndani adzalibweza? (Yesaya 14:26-27)

Yehova wa makamu ali ndi cholinga, ndipo balibe mphamvu ya dziko, thup, ziwana, Gehena, kapena Satana iye mwina sangachilepheretse. Inu muli tsopano m'bali yimodzi ya cholinga cha

uzimu kudzera mu utumiki wa kupembedzera. Tikutseka ndi mafotokodzedwe amphamvu a kupembedzera ofotokodzedwa ndi Canon Liddon:

“Kodi ndizoonna kuti kupembedzera ndikungogwirizana chabe ndi chidzolowedzi ndi kuzimiririka? Anthu omwe anapempherapo zowona ayankhe.

Nthawi zina amafotokoza pemphero ngati kholo Yakobo amene analimbana ndi mphamvu yosaoneka yomwe imatha, osati pafupipafupi mumoyo wozipereka, mu nthawi ya usiku, kapena nthawi yam asana. Nthawi zina amanthauza kupembedzera kwa Paulo kolimbana kwatsopano.

Iwo ali, akamapembera, maso awo atalunjika pa kupembedzera kwakukulu mu Getsemani, pa mwazi omwe unakhetsedwa pansu mu chipsinjo chofuna kusiya ndi msembe.

Kulimbikira ndi kofunikira pa kupembedzera kopindulitsa...zikutanthauza kuti osati kumangolota koma kugwira ntchito. Ndi kudzera mu kupembedzera ndi pamene Ufumu wa Kumwamba uli wokangamizidwa, ndipo okangamirawo aukwatula ndi mphamvu.” – Canon Libbon

Kodi ndinu okonzeka kuzipereka?

MAYESO OZIYESA NOKHA

1. Lembani Vesi yotsogolera.

2. Lembani ndongosolo lanu lakapembedzedwe. Kodi muyamba liti? Kodi tsiku linalirilonse mwayikidza kuti muzipembera nthawi zANJI? Kodi mudzikapempherera kuti?

3. Kodi ndi mavuto ati omwe akambidwa mu phunzirori omwe mukuyenera kuti muwagonjetse kuti muyambe ndi kupitiriza kupemphera?

4. Kodi malemba kale ndondomeko yakapempheredwe? _____ ngati ayi, onani “Zoonjezera Pophunzira” za chaputalachi.

5. Koti mwazipereka nokha ku kupembedzera kwa tsiku ndi tsiku?

6. Ngati mulia abusa, m’phunzitsi kapena mtsogolera wagulo, lembani dongosolo la kapempheredwe yomwe ingakhudze mpingo wanu, ophunzira anu, kapena mamembala a gulu lanu mu pemphero logwirizana.

(Mayankho amafusowa aperekedwa kumapeto kwa bukuli)

ZOONJEZERA POPHUNZIRA

Awa ndi malangizo omwe angakuthandizeni kulemba ndongosolo la kapempheredwe.

GAWO LOYAMBA: ZOLEMBA ZOPHUNZIRIRA

Ikani zolemba zomwe muziphunzirira za kupembedzera ndi kutsala kudya mu gawo iri ndicholinga choti mutha kuziwonanso mwakawirikawiri.

GAWO LACHIWIRI: MZINDA, DZIKO

Pedzani mapu a mzinda ndi dziko lanu kuti mudzipempherera. Pedzani mayina a adzitsogoleri a ndale ndi achipembedzo ndipo mudziwapempherera potchula mayina awo.

GAWO LACHITATU:

Pedzani ndondomeko ya zosowa za banja lanu, abwenzi lanu, ndi anthu ena ndipo zipembedzerani idzi tsiku ndi tsiku. Lembani mapemphero omwe ayankhidwa kuti adzikulimbisani mtima.

Mpingo wanu: Pedzani mayina a adzitsogolero a mpingo ndipo mudziwapempherera tsiku ndi tsiku. Pemphererani membala wina aliyense wa mpingo wanu pomawatchula mayina awo.

Utumiki wanu: Pembedzerani utumiki wanu. Ngati muli m'busa, pemphererani munthu winaaliyense wa mumpingo wanu potchula dzina lake. Ngati muli kholo, pemphererai ana anu (amene ali gawo la utumiki wanu). Ngati muli mvangeli, pempherani kuti makomo otumikira Utenga Wabwino atseguke.

GAWO LACHINAYI: KUPEMBEDZERA MAYIKO ENA

Mu gawo iri, pedzani malangidzo a utumiki wopembedzera mayiko ena omwe apatsidwa mu chaputala ichi. Muthanso kupeza mapu a mayiko osiyana siyana omwe mungaphatikidze mu gawo ino.

ZAKUMAPETO

ZAKUMAPETO 1: MAPEMPHERO A MU BAIBULO

Mwaphunzira mu phunzirori kuti Yesu ndi chitsanzo chachikulu cha pemphero lachitsanzo. Muli zitsanzo zina zambiri za opembedzera ochitachita mu Baibulo. Ndandanda wotsatirawu ndi zitsanzo za mapemphero amu Baibulo.

MAPEMPHERO AMU CHIPANGANO CHAKALE

Genesis:

Chiyambi cha mbiri ya pemphero: 4:26
Pemphero ndi kupita patsogolo mu uzimu: 5:21-24
Pemphero ndi guwa: 12-13
Pemphero, chilankhulo cha olira: 16
Pemphero ndi chibvumbulutso: 17
Pemphero la mzinda woyipa: 18-19
Pemphero lozichepesa: 22
Pemphero la mkazi wosaberka: 22:19-23
Pemphero ngati chipangano: 28
Pemphero la madalitso apa mitundu: 48-49

Eskodo:

Pemphero kuonetseredwa ngati kubuula: 1-2
Pemphero ngati kukambirana: 3-4
Pemphero ngati kudandaula: 5-7
Pemphero ngati matamando: 15
Pemphero la osowa: 22:22-24
Pemphero loyamba la Mose kw ana a Israyeli: 32:9;14
Pemphero lachiriri la Mose: 32:30-34
Pemphero lachitatu la Mose: 33:12-23
Pemphero ndi kuwalitsidwa: 34

Numeri:

Pemphero ngati m'dalitso: 6:24-27
Pemphero lochotsa chiweruza: 11:1-2
Pemphero la mtima waulesi: 11:10-35
Pemphero la mtima wofasa: 12
Pemphero ndi uneneri: 23-24
Kupempherera tsogoleri wa tsopano: 27

Deuteronomo:

Pemphero la ntchito yokonderedwa: 3:23-29
Pemphero kwa munthu amene ali pafupi: 4:7
Pemphero la madalitso: 21:6-9
Pemphero lachiyamiko: 26
Pemphero ngati nyimbo: 32-33

Yoswa:

Pemphera nngati chiphinjo: 5:13-15
Pemphero imene Mulungu sayankha: 7
Pemphero limene limabweretsa chozizwa: 10

Oweruza:

Pemphero yachitsogodzo: 1
Pemphero mu nthawi ya nkondo: 2-5
Kupempherera mwana amene sanabadwe: 13
Pemphero pokomana ndi imfa: 16:28-31
Kupempherera mtundu wotayika: 21:2-3

1 Samueli:

Pemphero lopada mawu: 1
Pemphero, lamaonekedwe a uneneri: 2:1-10
Pemphero lofuna mfumu: 8
Pemphero la mtima osweka: 15:11
Pemphero lobwezeretsa: 30

2 Samueli:

Kupempherera zizindikiro za chipambano: 5:19-25
Kupempherera mdalitso pa nyumba ndi ufumu: 7:18-29
Kupempherera mwana wodwala: 12
Pemphero ngati salimo: 22

1 Mafumu:

Pemphero lozipereka: 812-61
Pemphero la kuuka kwa mwana wakufa: 17:20-24
Pemphero la imfa: 19

2 Mafumu

Kupempherera mwana wa kufa: 4:32-37
Kupempherera masomphenya: 6:13-17
Kupempherera moyo wautali: 20:1-11

1 Mbiri:

Pemphero la chuma chazimu: 4:32-37

Pemphero la mantha: 13:12

Pemphero loyankhidwa ndi moto: 21

Pemphero ndi kupereka: 29:10-19

2 Mbiri:

Kupemphera pamene dziko liri pachiopsezo: 14:11

Pemphero lolapa: 33:13

Ezara:

Memphero la chiyamiko: 7:27-28

Pemphero ndi kusala kudya: 8:21-23

Pemphero ndi kuvomereza: 9:5-10:4

Masalimo:

Pemphero la chiyero: 4

Pemphero la mtanda: 22

Pemphero la chisamaliro cha m'busa: 23

Pemphero lowonetsera ulemerele wa umulungu: 24

Pemphero la mtima wokhulupirira: 27

Pemphero la chitetedzo: 35

Yeremiya:

Pemphero lochokera ku ndende: 6

Pemphero kukanizidwa: 7:16

Amosi:

Pemphero la kukhululukira: 7:1-9

Yona:

Pemphero lotuluka ku Gehena: 3

Pemphero la mzinda wolapa: 3

Pemphero la mneneri wokhumudwa: 4

MAPEMPHERO A MUCHIPANGANO CHATSOPANO

Mateyu:

Pemphero ndi kufunikira kwa kukhululukira: 5:22-26; 6:12,14-15

Pemphero ndi chinyengo: 6:5-7

Pemphero monga momwe anaphunzitsira Yesu: 6:8-11

Pemphero mu fanizo: 18:23-25

Pemphero la chikhulupiriro: 21:18-22
Pemphero lonamidzira: 23:14,15
Pemphero pa Kavale: 27:46,50

Marko:

Pemphero la chiwanda: 1:23-28,32-34
Prayer – Chikhalidwe cha Khristu: 1:35; 6:41,46
Kupemphera ndi kusala kudya: 2:18; 9:29

Luka:

Pemphero la Zakariya: 1:8,13,67-80
Pemphero ngati malambiro: 1:46-55
Pemphero ndi ophunzira khumi ndi awiri: 6:12-13.20,28
Pemphero mu fanizo: 11:5-13
Pemphero la mwana wolowerera: 15:11-24,29-30
Pemphero la akhate khumi: 17:12-19
Pemphero la mfalisi ndi okhometsa misonkho: 18:9-14
Pemphero ndi Ambuye owukitsidwa: 24:30,50-53

Yohane:

Kupempherera mzimu: 4:9,15,19,28; 7:37-39; 14:16
Pemphero la Mkate wa Moyo: 6:34
Pemphero ngati mwayi: 14:13-15; 15:16; 16:23-26
Pemphero la mapemphero onse: 17

Machitidwe:

Pemphero mu chipinda chapamwamba: 1:13-14
Pemphero ndi kulambira: 2:42-47
Kupempherera kulimbiki mtima pa kuchitira umboni: 4:23-31
Pemphero la ophedwa woyamba: 7:55-60
Pemphero la Koneriyasi: 10:2-4,9,31
Kupempherera Petro ali mu ndende: 12:5,12-17
Kupemphera ndi kusala kudya: 13:2-3; 14:15,23,26

Aroma:

Kupempherera ulendo wabwino: 1:8-15
Pemphero lowuziridwa mpeya ndi Mzimu: 8:15,23,26-27
Pemphero ngati utumiki wopitirira: 12:12
Pemphero logonjetsa Satana: 16:20,24-27

2 Akorinto:

Pemphero la mdalitso: 1:2-4
Kupemphera kuti minga ichotsedwe: 12:7-10

Aefeso:

Pemphero ndi cholowa cha okhulupirira: 1:1-11
Pemphero ngati njira yakwa Mulungu: 2:18; 3:12
Pemphero la kukwaniritsidwa kwa mkati: 3:13-21

Afilipo:

Pemphero ngati pempho la chimwemwe: 1:2-17
Pemphero ndi mtendere wa mu mtima: 4:6-7,19-23

Akolose:

Pemphero ngati matamando a kukhulukpirika: 1:1-8
Kupempherera madalitso asanu ndi awiri: 1:9-14
Chiyanjano cha pemphero: 4:2-4,12,17

1 Atesalonika:

Pemphero lakukumbukira: 1:1-3
Pemphero, matamando ndi ungwiro: 5:17-18,23-24,28

2 Atesalonika:

Pemphero la kutonthoza ndi kulimbitsa: 2:13,16-17
Pemphero la mawu ndi chitetedzo: 3:1-5

2 Timoteo:

Pemphero la utumiki wa Timoteo: 1:2-7
Pemphero la nyumba ya Onsesifolusi: 1:6-18
Pemphero la abwanzo onyenga: 4:14-18

Ahebri:

Pemphero lotamandira chirendedwe: 1:10-12
Pemphero la chisomo ndi chifundo: 4:16
Pemphero ndi utumiki wa Khristu: 5:7-8; 7:24-25
Pemphero la ungwiro: 13:20-21

Yakobo:

Kupempherera nzeru: 1:5-8,17
Pemphero imene imaphonya kofikira: 4:2-3
Pemphero limene limachita: 5:13-18

1 Petro:

Pemphero lachiyamiko pa cholowa: 1:3-4
Kupemphera ndi kuyang'anira: 4:7
Kupempherera kukhazikika kwa Akhristu: 5:10-11

2 Petro:

Pemphero lakuchulukitsa kwa chisomo ndi mtendere: 1:2

3 Yohane:

Pemphero la madziko a chikhalidwe chabwino: 1-4,12

Yuda:

Pemphero la muuzimu: 20

Chibvumbulitso:

Pemphero ngati matamando ku mwana wa Nkhosa: 5:9

Pemphero la akulu akulu: 11:3-4

Pemphero la Mose: 15:3-4

Pemphero la oyera mtima aulemerero: 19:1-10

Pemphero lothera Baibulo: 22:17,20

(Mapempherowa atengedwa kuchokera mu “Mapemphero onse a m’Baibulo” yolembedwa ndi E.N. Bounds)

ZAKUMAPETO 2

NDONDOMEKO YOPHUNZIRIRA: KUPEMBEDZERA KWA M'BAIBULO

Chitsanzo cha malembo cha pemphero: _____

Kodi anapemphera pemphero limeneri ndi ndani? _____

Mbiri ya munthu yaperekedwa mu zitsanzo zotsatirazi:

Makhalidwe abwino otsimikidziridwa mu moyo wa munthu wopembedzerayu:

Lembani makhalidwewa zomwe zikumupangitsa kukhala opemphedzera wabwino. (Izi ndi zinthu zimene mukuyenera kutenggera mu moyo wanu):

Makhalidwe omwe Sali abwino a mu moyo wa munthu wopembedzerayu:

Lembani makhalidwe omwe akupangisa kukhala opembedzera yemwe sali wabwino (Izi ndi zinthu zimene simukuyenera kutengerapo):

Kusanthula pemphero:

Kodi ndi zinthu ziti zimene zinamupangitsa munthuyo kuti apemphere?

Kodi pemphero likulunjika kuti?

Kodi ndi zopempha zANJI zimene zapemphedwa mu pemphero?

Kodi ndi mbali yoti ya pemphero lomwe liri lopembedzera? Kupempha? Kulapa? Kulambira ndi matamando?

Kodi muli chitsimikizo cha chikhulupiriro kapena kusowa chikhulupiriro mu pempherori?

Kodi ndi malembo ati omwe anenedwa mu pemphero?

Lembani malonjezano omwe atchulidwa mu pemphero?

Kodi pemphero linayankhidwa? Liti? Bwannji?

Ngati sirinayankhidwe, chifukwa chani?

Kodi zotsatira za pemphero zinali zotani?

Kodi inu mungaphunzire zotani mu pempherori kuti mapembedzero anu akhale ochitachita?

MAYANKHO AMAFUNSO OZIYESA NOKHA

CHAPUTALA 1:

1. Pemphani, ndipo cidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani, ndipo cidzatsegulidwa kwa inu; pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo citsegulldwa. (Mateyu 7:7-8)
2. Pemphero ndi kulumikidzana ndi Mulungu. Imatenga njira zosiyana siyana koma imachitika pomwe munthu akulankhula ndi Mulungu ndi Mulungu kulankhula ndi munthu.
3. Baibulo limaonetsera ku pemphero limayankhidwa:
Nthawi zina pompo pompo: Yesaya 65:24; Danieli 9:21-23
Nthawi zina limachedwerapo: Luka 18:7
Kutsiyana ndi zokhumba zathu: 2 Akorinto 12:8-9
Kupyola zoyembekedera zathu: Yeremiya 33:3 Aefeso 3:20
4. Pali milingo itatu ya pemphero: Kupempha, kufuna, ndi kugogoda. Kupempha ndi mlingo woyambirira wa pemphero. Kumatanthauza kupereka zopempha kwa Mulungu ndi kulandira yankho pompopompoKufuna ndi mlingo wakuya wa pemphero. Kugogona ndi mlingo wakuya. Ndi pemphero lomwe liri lokakamidza ngati yankho silikubwera

CHAPUTALA 2:

1. kucokera komwekoakhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Mulungu mwa iye, popeza ali nao moyo wace cikhalire wa kuwapembedzera iwo. (Ahebri 7:25)
2. kupemphedzera kutha kutanthauzidwa ngati pemphero langwiro, lakhama lomwe munthu amadandaulira Mulungu m'malo mwa munthu wina kapena anthu ena omwe akufunikira kupedzeka kwa Mulungu.
3. Maziko athu a m'Baibulo mu utumiki wa okhulupirira a Chipangano Chatsopano wa pemphero lopembedzera ndi mayitanidwe athu ngati ansembe akwa Mulungu. Mawu a Mulungu amalengedza kuti ndife ansembe oyera mtima (1 Petro 2:5), mbadwa wosankhidwa (1 Petro 2:9), ndi ufumu wa ansembe (Chibvumbulutso 1:5).
4. Yesu Khristu.
5. Ngati opembedzera omwe tikusatira kagwiridwe ka ntchito ka ansembe a Chipangano Chakale ndi ndondomeko ya Chipangano Chatsopano cha Yesu, timayima pamaso pa Mulungu ndi pakati pa Mulungu ndi munthu wauchimo.

6. Kupembedzera ndikofunika kwambiri chifukwa cha kutsindikiza komwe Yesu anayika pa iwo pa utumiki wake wa dziko lapansi. Kufunika kwake kunalembedwanso mu Baibulo omwe umakwaniritsa nkhani za anthu omwe anakumana ndi zotsatira zamphamvu kudzera mu kupembedzera kochitachita.

CHAPUTALA 3:

1. Ndipo iye anaitana pamodzi khumi ndi awiriwo nawapatsa mphamvu ndi ulamuliro pa ziwanda zonse, ndi zakuciritsa nthenda. (Luka 9:1)
2. Ulamuliro wanu pa m'dani umachokera kudzera mwa Yesu Khristu ndi udindo womwe muli nawo mwa Iye ngati okhulupirira. Mphamvu yanu pa m'dani imachokera kwa Mzimu Woyera.
3. Mawu oti “kumanga” amachokera ku mawu achi Heberi oti *osar* kutanthauza “kumanga, kuyang'anira.” Mawuwa timawagwiritsa ntchito powonetsera kumanga mahatsi ndi mabulu (2 Mafumu 7:10).
4. Kumasulu ndi kuchosa mu ukapolo. Mutha kumasula amuna ndi akazi ku nsinga za tchimo, maganizo, ndi kukhumudwitsidwa ndi m'dani.
5. Mateyu 16:19
6. Dzina la Yesu ndi la mphamvu chifukwa ndi ulamuliro omwe ife timapembedzerapo pamso pa Mulungu. Onani Yohane 14:14
7. Kudzera mu mzawi wa Yesu ife tiri ndi mwayi wofika pamaso pa Mulungu Atate. Onani Ahebri 10:19-23
8. Kusala kosadya kapena kumwa kalikonse. Chitsanzo cha ichi chikupezeka pa Machitidwe 9:9. Kusala kwapadera ndi pamene chakudya china sichikudyedwa. Chitsanzo cha ichi chiri pa Danieli 10:3.
9. Kusala kudya sikusintho Mulungu. Kumasintho inuyo. Mulungu amakhala nanu malingana ndi ubale wanu ndi Iye. Mukasintho, momwe Mulungu amagwirira ntchito ndi inu kumasintho. Simumasala kuti mukasintho Mulungu chifukwa Mulungu sasintha.
10. Yesaya 58 akufotokoza za kusala kosankhidwa ndi Mulungu.
11. Mukamasala, chinthu choyamba chimene chimachitika ndichakuti Mulungu amayamba kuzibvumbulutsa yekha kwa inu. (Yesaya 58:9).

CHAPUTALA 4:

1. Ndipo uku ndi kulimbika mrima kumene tiri nako kwa iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa cifuniro cace, atimvera; ndipo ngati tidziwa kuti atimvera ciri conse ticipempha, tidziwa kuti tiri nazo izi tazipempha kwa iye. (1 Yohane 5:14-15)
2. Onanitso awo ya m'mene mungapembedzerere mu Chaputala 4.
3. Mu Chaputala 4, onanotso gawo la zomwe tingapembedzere mu pemphero.
4. Onanitso mfundo za kupembedzera kochitachita mu Chaputala 4.
5. Mumahanzira zomwe Mulungu walonjeza ndipo pempherana molingana ndi malonjezanowa. Njira imodzi yochitira izi ndikupita mu Baibulo ndikulunjika pemphero lanu molingana ndi malonjezanowa.

CHAPUTALA 5:

1. Mupempha, ndipo simulandira, popeza mupempha koipa, kuti mukacimwaze pocita zikhumbitso zanu. (Yakobo 4:3)
2. Tchimo la mtundu wina uli wonse; Mafano amu mtima: Kuzikonda, zolinga zolakwika: Njala ulamuliro: Kukhala bwino ndi apabanja anu: Kuziyelesa nokha: Kusakhulupirira: Kusakhala mwa Khristu ndi mu Mawu Ake: Kupempha kosiyana ndi chifuniro cha Mulungu: kupempha osagwiritse ntchito dzina la Yesu: Zolepheretsa za ziwanda: Pamene simukuziwa momwe mukuyenera kupempherera, pemphereo limalepheretsedwa.
3. Pemene Mulungu wakuuzani kuti muchite chinthu. Musagwiritse ntchito kupembedzera ngati njira yothawira kuchita zimene Mulungu wakuuzani kuti muchite.

CHAPUTALA 6:

1. Atate wathu wa Kumwamba,
Dzina lanu liyeretsedwe.
Ufumu wanu udze.
Kufuna kwanu kucitidwe,
Monga Kumwamba comweco panso pano.
Mutipatse ife lero cakudya cathu calero.
Ndipo mutikhululukire mangawa athu,
Monga ifenso takhululukira amangawa anthu.
Ndipo musatitengere kokatiyesa,
Koma mutipulumutse kwa woipayo.
Chifukwa wanu ndi ufumu, ndi mphamvu ndi ulemerero wa nthawi zonse. Amen.
(Mateyu 6:9-13)
2. Mateyu 6:9-13 ndi Luka 11:2-4.

CHAPUTALA 7:

1. Ndipo anthu anga ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhulukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao. (2 Mbiri 7:14).
2. Ntchito za umulungu zodabwitsa za Mulungu zodzera ndi m'malo mwa anthu omwe aphunzira ndi agwirotsa ntchito mfundo za Mawu a Mulungu a rhama okhudzana ndi chitsitsimutso.
3. Tikuyenera kukonzekera pakutsata mfundo za chitsitsimutso zomwe zawonetseredwa mu Mawu a Mulungu. Chitsitsimutso ndi kugwirizana kwa kuyenda kwa Mzimu Woyera ndi kuvomereza kwa anthu a Muungu.
4. Chitsitsimutso chimafunikira pamene kubwerera m'buyo kukuonekera.
5. Fananizani mayankho anu ndi zizindikiro za chikhalidwe chobwerera m'buyo zimene zaperekedwa mu Chaputala 7
6. Fananizani yankho lanu ndi mfundo za m'Baibulo za chitsitsimutso zomwe zaperekedwa mu Chaputala 7.
7. Onani zokambirana za Chaputala 7
8. 2 Mbiri 7:14
9. Zichepeseni; Pempherani; Funani nkhope Yake; Katembenukeni ndikuleka njira zoipa. Onani zokambirana za Chaputala 7

CHAPUTALA 8:

1. Koma iwe popemphera, lowa m'cipinda cako, nutseke citseko cako, nupemphere Atate wako ali m'tseri, ndipo Atate wako wakuona m'tseri adzakubwezera iwe. (Mateyu 6:6)
2. Mayankho asiyana.
3. Mayankho atha kukhala ndi izi: Kusowa kwa nthawi, zolepheretsa, kutopa, kusowa chikhumbokhumbo.
4. Mayankho asiyana.
5. Mayankho asiyana.
6. Mayankho asiyana.

